*Mu mpingo umene Yesu ama kuchita,*
*ndi kupanga zinthu, ndi mwa moyo,—osati mwa mbiri*
*yakale chabe ndi kuyamukilidwa ndi kusamalidwa mu*
*kuphunzitsa—muli ufulu!*

*Aliyense pamodzi ndi Yesu pokhala pamodzi ndi*
*kuchita motere, tsiku lililonse pakati paokhulupirira*
*ali ndi udindo kupeleka mphatso zawo*
*"pakumangilira thupi lonse"*
*Mu Mphatso Zake Zonse..*



# YESU

WOWONA ... WOSATI ONAMA
ZOONA... OSATI OYELEKEZA,
MUTU ... OSATI ZOPEKA.

Mwathawi yonse ngati mufuna thandizo mu munjira ina ili yonse lemberani kuno ku mpingo wa Indianapolis P.O Box 68309, Indianapolis, IN 46268 USA.

Kapena *www.Yesu-Kristo.com*

Mukjonza kuchulukitsa koma musagulitse mtengo wina uli wonse. (2 Akorinto 2:17, Mateyu 10:8).









# Konzekera Wekha Namwali Iwe!

Kuitana kwa Mulungu ku dziko lapansi ndiyo kmalo pamodzi ndi Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera—kukhala mkwatibwi wokonzeka kubwera kwa mkwatibwi wokongolayo, Yesu. (Yohane 13:15, Aefeso 2–5, Chibvumbulutso 19–7) ngati mukuganiza za chithunzi cha malembo mmene moyo, wa, kristu umakomanilana—uli bwanji? Yofunsilana—ndi madyelero a ukwati Mulungu atifunsa ife, ati, " Ndili nacho chiyembekezo ine. Ngati ukhala ndi ine, yanganila kuti ndine yani, palibenso wina ofanana nane. Palibe padziko lapansi amene adzakwanilitse moyo wako monga: ine—chifukwa ndinakulenga wa ine. Zina ndi zonse ndi zochotsera iwe, koma ngati ungathe kulowera mbali yanga, udzaona mmene moyo umayenela, ndipo tidzakhala pa ukwati."

*" Konzeka Mkwatibwi"*

Pachiyambi pomwe kuitana uku kwabweletsa anthu kufuna—funa iye. Ndiye kuitanidwa kwa ifenso ndiye m'mene zilili. Sichiphunzitso ai, ndi zimene zili mkati mwa ife. Tiyanganila zimene iye ali, ndi kulankhula. "Sindingathe kukhala popanda iye kapena kukongola ndi kufunika kotani kwa iye! Sindingathe kukhala popanda izi. Sindinalole kukhala kunja kwa malingaliro a moyo wanga ndi wa cholinga chake. Ndifuna kumutsata mwana wa nkhosa popita iye. Zonse zimene afuna ndi moyo wanga, apeza iye! Ndiye mkate wa moyo umene zoyenela zonse zipezeka ndi kukwanilitsidwapo mopezeka. Iye ndiye chithunzi cha utsogoleri, ndi kukoma mtima ndi kukhululuka ndi chifundo zimene sindingathe kukhala popanda izo! Ndifuna iye wamphamvu, iye wangwilo, iye wokoma mtima, iye wokonda ndi wachifundo. Iye wanzeru zosaneneka *NDIFUNA KUKHALA NDI IYE!* Ndimvetsele mau onse anena. Sindifuna kutalikana naye ai nthawi ya umoyo wanga. Sindimuonetsa msana chifukwa cha kudzikonda, ulesi, kapena kupwetekedwa mtima. Sindionetsa msana wanga kwa iye. Zoyesedwa zilipo koma zoonengeka zidzakhala zazikulu."

Yesu ali ndi kupambana, ali mukuchuluka mwa zikwi—zikwi munjira, nzeru zochuluka. Ali Ambuye iye ndi Yesu sinthano ai, si nkhani chabe za timilungu olenga dziko lapansi, okhala pampando wa chifumu oyera. Ndiza munthu otchedwa Yesu ndi Atate amene ali oweluza ife tonse. Ife ngati tingaone, ngati tikatenge nthawi kumudziwa iye, palibenso kumukanizanso kopitilira. Bvuto lakhala kupanda kufunitsitsa kuziletsa kumanja ake wotheka achikondi.

Kukhulupirika kwake ndikopanda malile. Koma sititha nthawi zonse kukhala pafupi mokwanila kuona, chifukwa cha ntchito yathu—yathu, kuzikonda, kusasamala–osakhala ndi nthawi naye kwenikweni.

Atate adziwa kuti ngati tikhala ndi nthawi ndi mwana wake, ndiye adzaonetsa khalidwe kwa ife munjira yomwe kwenikweni yotamandika. Zoyeneleza makhalidwe ake ali achipambano pali zina zomwe zili zokhala mwa iye zimene zingakutengeleni kunja



kwa zonse zomwe zikugwetsa inu pansi. Kenaka muyangana za kunja kwa dziko lomwe inu muli limene kukhala muzochitika Ameneyo ndi YESU! Waitana tonse kuyenda ndi iye. Iye adzaonetsa inu, kukoma mtima, chifundo, ndi kukhululuka kosatha.

Mudzaona kumwetulira mu maso ake. Mudzaona mmene mphepo iwombela pa tsisi lake. Mudzaona ndikumva zochitika kukutengelani inu kudziko lina mmene nthawi sipita. (Chivumbulutso 1:12–18) Mudzaona utsogoleri ndi mphamvu zake. Mudzaona mmene anagonjetsera uchimo. Mudzaona kuti iye ali ndi masomphenya eni—eni mmene moyo ungakhalire. Mudzamva kuzama kwa kusekelera ndi kumva kutentha kwa kulimbikisidwa kwake.

Londola iye. Adzakuonetsa utsogoleri, adzakuonetsa kulimbika. Adzakuonetsa khalidwe losasuntha ndi moyo wopambana umene udzaonekera pa iwe. Umene udzakutengela kwa iye, potetezedwa kumene iye akhalako. Adzakuonetsa mtima wabwino, ndi nzeru zoyangana mtima ndi moyo yomvetsa chisoni wako—wako—ndiye iye adzasambitsa, kuyeletsa, kulonga mzimu wake mwa iwe. Adzakupatsa mwala wa mtengo wapatali ndi miala yapamwamba imene kwa iye adzakupatsa zonse. Udzakhala mfumukazi, nudzakhala mfumu.

Akufuna kumanga usilikali pa otsatira ake-sinkhamwa chabe, zoganiza, zophunzitsa—"Idzakwa ine kapena mudzapita ku Gehena" chabwino, ndizoona. Koma sizilingana ndi zimene anadzaonetsa kwa ophunzira ake khumi ndi awiri, mukuganiza kuti amamutsata konse m'midzi chifukwa amaloza kwa iyo chala ndi kunena kuti tsatani ine Yesu, kapena adzapita ku chionongeko? Mukumbukira lembo liri lonse lonena chomwechi? Ndizimene anachita pamene anapita ndi kupemphera kw aAtate usiku onse? Anatelo kodi? "Atate, onetsani zimene ndinene" naima nati, "inu khumi ndi awiri, bwerani pamodzi nane, kapena, mudzapita ku chionongeko?

Ai, anafuna kukhala naye chifukwa anaona kanthu, mwa iye, kamene kanadabwitsa.

Anaona nzeru zake mtima wabwino ndi odekha. Adaona utsogoleri ndi makhalidwe yosatekeseka mwa iye. Anaona wina amene angatenge moyo ndi kuupambanitsa ndi pakamwa posekelera, pa nkhope pake ndi kulimbika mmaso mwake. Anafuna kukhala monga iye. Anafuna kukhala naye! Sakanapita kwina, chifukwa kunalibe kwina kumene anakakhala koposa kukhala pambali pake (Mateyu 4:19–22, Yohane 6:68, Machitidwe Atumwi 3:19–20)

Sanaopsyeze iwo, ndipo sakutiopsyeza ifenso. Iye ali kuitana ife tonse kuti tidziwe kuti iye ali ndani ndinso kuona kudabwitsa kwake ndi kudabwitsa pazochita zake kuti ali choncho kuti tikhale ndi iye, mu moyo wake ndi zina. Ine ndifuna kukhale ndi iye pamene ndidzakula ndi zoona ndinenazi.

Posachedwapa Yesu, abwera kwa Mkwatibwi yokonzekelayo. Cholinga cha Atate ndichoti, osati tilandire mkwati ai koma tikhale mkwatibwi osati tidzakhale mnyumba koma ndidzakhale nyumba. Tikabwelera mbuyo mu chipangano chakale, mudzaona kuti anali ofunitsitsa nyumba, osati kuombola anthu kuti akhale ndi zinthu. Anafunitsitsa kukhala nyumba, malo amene angakhale padziko lino limene analilenga. Yesu anati kwa ife mu Luka 17 kuti ufumu wake suli uko kapena pano, koma mwa ***anthu,*** *amene akulitsa malo mu mtima mwawo* kukana zinthu zadziko lapansi, zofuna za thupi, zilakolako ndi kunyada. Tiyenela kukhala amene takonza chipinda cha Yesu mumtima mwathu monga Yesu anatiphunzitsa mu Yohane 8. Awa ndiye makhalidwe a Mpingo, thupi lamoyo ndi mpingo.

Yesu sanangobwera kudzankhulukuka machimo, modabwitsa motero, kapena kudzatinganizitsa za ziphunzitsao zake. Yesu anabwera kuti potero ife tikhale ndi moyo omwe uli ndi Atate omwe iye anali nawonso—osangokhala chabe pano pa dziko, kufa, ndikupita kumwamba. Monga bukhu lopatulika linena, Anadza kuti ife tikhale mu mphamvu yopambanitsa mmoyo, mu moyo wa chiyanjano ndi moyo wa chikondi pamodzi ndi Atate ndi Abale amene ali nawo.



"Kuomboledwa" ndi mtunda yotalika kwa nkhani, monga mwa kubadwa kwa Yesu, kubadwa kwathu ndi chiyambi cha nkhani yopambana imene Atate afuna atiuze (Akolose 1:26–29, Agalatiya 4:19, Yohane 7:38) chikhumbo chake ndi choti Kristo atumphuke mwa ife, ndikuti ife (Anthu ake, Mkwatibwi wake, nyumba yake, mpingo wake) uwonetsele ulemelero wake wa Yesu wa ku Nazarene pa dziko lino lapansi mu nyengo ino. Atate safuna chabe munthu payekha powonetsela Yesu, koma PAMODZI, mogwilizana, tikhale chenicheni choimilira iye Yesu.

Ndi pogwila ntchito yotele "Chuma chobisika" chili ndi zonse zamoyo mmene tikhalira pamodzi tsiku ndi tsiku. Zimene chipembedzo ndi chikristo chachita kwa zaka zambili mukuphunzitsa za Yesu ndi mpingo. Ndi nthawi yopita pa tsogolo kuchoka mu chiphunzitso *cha* zampingo kuti *tikhale* mpingo (Aefeso 3:10, Mateyu 16:18).

Tingakhale ife Mpingo ndi kukhala moyo monga tikondana wina ndi mzake ndi kusinthana wina mmoyo tsiku ndi tsiku. Tithandizana wina ndi mnzake kuziwa bwinoYesu, pothandizana wina ndi mnzake kutchosa chimo, kukondana koposa, ndi pothandiza ena zosowa zawo kuposa monga tingazithandize tokha.

Izi ndi chiphunzitso cha Yesu umu ndi mmene akhalira moyo wake mwa ife, ndiyo watiitana tsopana kukhala mnjira yotere kwa wina ndi mnzake. Umu ndi mmene mkwatibwi "wakonzekera" pobwera kwa mkwati, yesu. Tidzakhala okongola mopambana pamene titchosa kuzikonda ndi kunyada kumene kumatichotsa ife ndi mzake, ndipo pamene ife tafunitsitsa kutsegula moyo kukhala ofunikira kwa aliyense, choncho Mzimu wa Ambuye, chisomo cha Ambuye ndi chikondi chizagwa pa ife—ndi kukhala mkwatibwi okongola okonzeka kubwela kwa mkwati Yesu.

Uwu ndi mpingo—okhala motere tsiku lililonse, osati kuonelera mu nyumba ya Mulungu, koma kukhala malo amene Mulungu akhalamo.

Choncho makomo athu, malo atchito ndi mpingo onse pamodzi. Palibe zotchinga mumtima wanga kwa ena ndiponso zotchinga pakati pa nyumba yanga ndi zanu. Ndichotsa kuzikonda kwanga, kunyada, ulesi, kusakhulupilira ndi kukonda ena monga Yesu andikondela ine. Pamene tonse titelo, kuchokera wang'ono mpaka wa mkulu, Yesu athira mafuta ochilitsa ndi ife tonse mpingo, mkwatibwi okongola. Yesu sanadze kudzatiika ife aukhondo. ***Anadza kudzatipatsa moyo wochuluka—kukhala moyo nthawi yonse ndi anzathu, osalankhula mau obweleka ndi kuimba ndi kupemphela mau a chipembedzo. MOYO!***



# YESU:
# *Omanga ndi Mmisili*

## Kumanga ndi Milimo
*Mpingo ndi chiani ndi Mkristo?*

Baibulo limatiphunzitsa kuti Mulungu sakhala nyumba zomangidwa ndi manja a anthu. Aefeso 2 ndi mbali zina za Baibulo zimati ife ndife malo okhalamo Mulungu mwa mzimu—mpingo. Pamene muyenda kapena kuyendetsa pa mseu, mukhoza kuzindikila zomanga za chipembedzo chifukwa ndi zooneka motelo, koma, poti mpingo weniweni ndi omangidwa mwa anthu, osati zomanga, ndiye umaoneka motani? Mungazindikile bwanji mpingo oona ndi onama?

Mumpingo wachipangano chakale, umakhala membala chifukwa choti makolo ako ndi (Ayuda) ngati umakhulupila chinthu chabwino ndipo makolo ako ali mbali ya mpingo, ndiye, iwe "umakhala mu mpingo" nthawi zonse, ndi kupeleka chakhumi, pamenepo inu mumakhala a mu 'mpingowo'.

Mumpingoyo *chipangano chatsopano wa Yesu, zimenezi sizoona.* ***Muyenela Kupeleka Moyo wanu kwa Mulungu.*** Uneneli wa mu chipangano chatsopano umati kuti mpingo umene Mulungu akumanga (Yeremiya 3, Aher 8, Heb 10) ndiwo mpingo weniweni owona, umene ang'ono mpaka akulu onse *adziwa Mulungu* mpingo ungadziwike mu njira imeneyi. Kuchotsela apa ndi chipembedzo chabe (chokhala chimene opumulitsidwa achita chabe) koma osati ndi mpingo oona wa Yesu Kristo choikapo nyali, ngati ali anthu achita ndi kuonelela chimene chilli kale osati kulumikizidwa kwa moyo pamodzi (1 Akolinto 12)

Mpingo oona omangidwa ndi miala ya moyo umene Yesu amaiona, naikonda iyenela yopangidwa ndi zisulo zabwino. Ngati nyumba imangidwa ndi zitsulo zosalimba, mudziwe kuti idzagwa ngati mitengo wogwilizitsila ndi yoola, idzagwa pansi. Njerwa zofewa zosaumbidwa bwino, kapena zopangidwa ndi zosalimba sizingathe kuthandiza kulemela kwa denga ndipo idzagwa. Monganso, ngati tiyesa kumanga nyumba ya Mulungu muzomangila zosalimba, idzagwanso ndithu ngati munthu sadziwa Mulungu, sangakhale otsatila mpingo wa Yesu ngati nyumba imene Mulungu akumanga kuchokera kwa Amuna ndi Amayi idzakhale yotheka kuima, siiyenela kukhala miala yoipa pa nyumbayi. (1 Akorinto 3 : 3–5).

Koyenela mpingo, kapena onse pamodzi, potero opanda chilema? Inde sizophweka ayi (1 Yohane 1) koma kolingana ndi mau a Mulungu, chofunikila ndi ichi: onse ochuluka mwa abale—"akonde kuunika" "akonde choonadi" ndipo akhale kuona mtima kwenikweni mwa Mulungu mu njira imene "thupi ndi mwazi—sizinaulilire" inde, ndizo zofunikira (Mateyu 16:16–18, Yohane 3:19–21, 1 Yohane 1–3, Eze 11:19, Yeremiya 31:34, Eze 36:26) Zimenezi ndi zimene Yesu anati adzamanga mpingo wake pamenepo, ngati uli wakedi. Zina zake zidzakhala ngati kumanga pa nyumba ndi njerwa zosalimba kapena matabwa mu dziko lapansi, ndipo Yesu adzagwilitsa mitengo woona pomangila nyumbayi.

Kenanso aka kuti sikuti munthu aliyense ali wabwino. Koma, zithandauza munthu, akonde ndi kumvera Yesu ndipo sanyosera kuthandiza kwa ena, amene afuna kuthandiza iwo kukonda ndi kumvera Yesu, afuna kuthandizika zomangila zabwino za nyumba ya Mulungu ndi pamene munthu amene safuna chithandizo iye amati, " osandiweluza ine" "samala zako amaziteteza," "chotsa choipa m'maso mwako" zimenezo ndi zomangila zoipa, zimene Mulungu salora mnyumba yake. Yesu sadzamanga nyumba yake motelo. Iyi ndi mitengo wowola ndipo udzadulidwa pakati pa anthu. (Machitidwe 3:23, Mat 18, 1 Akorinto 5) Mu mpingo woona amene atelo saloledwa. Ngakhale atakhala ndi ndalama zochuluka, kapena amadziwa Baibulo motani angakhalenso mtsogoleri" koma ngati sabvomeleza mpingo wa Yesu mofewa ku chiphunzitso cha



Yesu, ndiye sangakhale ku mbali ya mpingo woona umene uchitika mu mzimu. Ngati akana, chikondi ndi kupepsa nzeru, kuthandiza ndi kudekha mtima, ndi kuwalola kukhala pakati pa abale ndiye tikutsutsa Yesu ngakhale malamulo ake.

Ngati wina ndi woomboledwa, ayenela kukhala ndi Mzimu woyela (Aroma 8:9, Agalatiya 3, Aefeso 1) ndipo kudziwa kuti ali ndi Mzimu Woyela mwa iwo (angakhale ndi umboni otani ndi kuti, "Ambuye" Mateyu 7) amakonda kumvela. Ali olengedwa atsopano ndikukonda kuwala ndi kukonda choonadi

(2 Atesolonika 10) ndipo monga "makanda obadwa kumene" ***amakhala ndi mau a Mulungu kuchitidwa mu moyo wawo*** (1 Petro 2) ngati munthu ali ndi Mzimu wa Mulungu amakonda kuunika ndi choonadi, ndipo makhalidwe awo amayamba kusintha. Amalapa mmene amakhalila ndi akazi awo kapena amuna awo, ndipo amasinthikadi. Amasintha mmene amakhalira ndi antchito awo, kapena ana awo, anzawo azungulila nyumba zawo, ndipo amasintha. amalapa machimo awo akale ndi makhalidwe oipa amasinthadi, ndi kukula msinkhu.

Mphatso ya mzimu oyera ndilo dipo la cholowa chawo "chinthu ndiwo cholamulidwa chawo" atero Yesu, mu Yohane 3. Ichi ndi chimene chimasiyanitsa olungama kuchionongeko. Sikuti onse ndi olungama, koma iwo amene akhululukidwa onse. "Akonda kuwala, ali ndi mphatso ya Mzimu woyera umene adalibe kale. Tsopano kuchokela pansi pa mitima ya mwala, yakhala ofewa kuchokela pansi pa mitima ya mwala, yakhala ofewa kuchokela pansi pa mtima, Mulungu wapangitsa kumvela malamulo ake. Kuchosela pansi pa mtima amasamala mau a Yesu pa makhalidwe. Nkhosa zimamva mau a Mbusa chifukwa ali ndi mzimu wa Yesu.

Nkhosa inena "ine ndifuna Yesu! Ndilondolereni ine njira imeneyo." Mbuzi inena, "ndisiyeni ine ndekha! Ndikhoza kuchita chozizwa! Ndikhoza kupereka ndalama zanga kwa aphawi! Ndimadziwa zinthu ndekha. Ine ndili bwino kuposa inu, ndipo sindisamala zomwe munene."

Mukhristu, ogawana nawo wa pangano latsopano, akonda chilungamo (2 Atesalonika 2:10) ndipo akonda kuwala (Yohane 3:19–21), ndipo tsopano ndi ogawana nawo chilengedwe cha Uzimu" (2 Peter 1:4, Aroma 6:1–14). Icho ndicho chizindikiro choti Mzimu ukhala mwa iwo kapena mwa aliyense waife. Ife sitiyenera kulenga mau a wina aliyense poti chifukwa anena, "Ambuye! Ambuye!" ***Yekha munthu amene azitaya yekha ndipo amoyo kwa Yesu ndi kuti iwo anena akhudzidwa ndi kumwamba ndipo akhala mwa mulengi wa dziko ali opulumutsidwa mowonadi ndi "membala" wa Mpingo wake*** (Aroma 8:9–11, Luka 9:57–62, Yohane 1:12–13, 3:16–21, 1 Yohane 3:8–10, 5:18–20).

Choikilapo nyali chenicheni mu chowonadi, mpingo weniweni uli ndi malire ("monga muzikwi zikwi wa mamembala!") kwa iwo akhala ndivumbulutso la mwana "kuti thupi ndi mwazi sizidavumbulitsa, koma Atate yekha kumwamba wavumbulutsa kwa iwo." Sizokhudza chifupi, kapena chidziwitso kapena kuzipereka kapena kukulitsa. Ndidzakhudzana ndi kukumana ndi Mulungu tate, mu umunthu wa Mwana wake, pamene imfaibala moyo onga wa Mulungu watunthu kuchoka popanda kanthu (Yoha 3:5–8, 12:24, Aroma 6:1–14, Agalatiya 6:14–17) ndi zoonadi alipo ena ochepa amene afuna chobvala ndi enanso amene akuganizira mwa " chaka chonse" chawo (Yoh 13:8–9, Yoh 15, Yoh 2:19, Yuda 11–25)

Ife mwina tili ndi moyo wodabwitsa ndi iye ndiponso ndi wina ndimnzake, kapena si—Ukhristu wolembedwa m' Baibulo ndi silili mpingo wolembedwa. Indetu alipo anthu ena opulumutsidwa amene akhala m'magulu amene siali mipingo yoonadi, ngakhale adzitcha okha mipingo. Iyo ndinkhani yinanso ife tikunene kuti sitikhudza mpando wake wachifumu (ife tingokhuzako umunthu wathu ndi kuzitenthetsa ngati ife sitikhala pamodzi m'moyo wapamwamba wa Mulungu). Nthawi ndi nthawi kulumikizidwa ku mutu ndi kwawina ndi mnzake! Mwambo umene "uchitika popatsa iye ulemu wake" kapena kuti tiphunzire mfundo za iye, kapena kuti tiyitane zofuna za thupi kuchokera kumwamba ndi nyimbo zathu—mwa ngati mbiri,



izi zasintha miyoyo yochepa chabe mwa chithudzi cha Mwana. Ife mwina tikugawana mu zinthu za Umulungu pamodzi tsiku ndi tsiku, kapena simoyo wosatha ayi, kapena choyimikira nyali ndi mpingo, ngati mmene Mulungu adachipangira. " chotupitsa chochepa chitupitsa mkate WONSE."

Ife tisakhale ngati makanda amene amanena zinthu zoona, koma sakhala ngati Yesu. Ndipo, mpingo simsonkhano wa onga akhristu amene amanena zinthu zoona koma alibe Mzimu wa Yesu mkati mwawo, ngati munthu. Yesu ndiwomanga wamkulu. Iye sadzamanga ndimwala wofewa ndi thabwa lovunda ayi. Iye afuna kumanga nyumba ya ulemelero kukhalamo yoyenera mfumu imene iye ali. Tsono mitengo yomangira nyumba ya Mulungu uyenera kukhala wabwino. Mpingo woona opangidwa ndi Mulungu osati ndi manja a munthu, opangidwa kuchokera ku miyala yamoyo—Akristu woona—zotsutsana ndi miyala yakufa, kapena njerwa. Yesu amanga ndi miyala yabwino yokha.

Ngati ife takwatirana ndi iye mu pangano ndi lumbira. Kuyisa zikonda zina zonse, kubadwanso kachiwiri, kukhala ndi mitima yofewa, kukonda ziphunzitso zake, kufunitsa kusintha zinthu zofunika kusintha m'moyo wathu. Ndikutembenuza nkhope yathu kwaiye munthawi yazovuta kapena zophinja, kufunsa iye ndi abalendi alongo athu kuti atithandize, ndiye kuti tili mwala wokongola wa moyo wa nyumba yoti Yesu akhalemo. Ungakhale ndipo idzakhala mkwatibwi waulemelero wa Yesu. Uwu ndiye uthenga wabwino wa Ufumu wa Mulungu.

## Kumanga Ndi Mapangidwe Ndi Mamangidwe A

### *Moyo wa Tsiku ndi Tsiku Pamodzi*

Tsopano poti tatanthauzira / fotokozera chimene chilli zomangira zabwino kumangira nyumba ya Mulungu… Nganizilani ichi: Tingoyesera tatenga miyala yonse yabwino, matabwa onse abwino, ndi zonse zabwino, zoyenera kumangira zimene Yesu wasankha za nyumba yake ndikuziunjika zonse zomangira

zabwinozo pamodzi. Chingachitike nchiyani, ganizani? Nyumbayo pakadalibe, sindinamange. Nyumba ya Mulungu imafuna kupyola pa katundu womangira wabwino (Akhristu owona). Chifukwa choti uli ndi zonse zofunikira pomanga nyumba zounjikidwa pamodzi sizitanthauza kuti uli ndi nyumba yogonamo ayi. Mulu wa zinthu zomangirawo sungakupulumutse ku namodwe, ngakhale zitakhala zabwino chotani.

*Kuti ikhale nyumba yabwino kuli Yesu akhalamo, nyumba ya Mulungu iyenera kumangidwa pamodzi kugwiritsa* ***kamangidwe*** *ndi* ***kapangidwe*** *ka iye. Nyumba yake ndiyopangidwa ndi anthu,* ***miyala ya moyo wake,*** *ndipo* ***Ali ndi njira yomwe tingamangire miyoyo yathu pamodzi.*** *Malembo amutcha Yesu omanga Wamkulu. Ife tiyenera kusamalitsitsa za makonzedwe a Iye.*

Mulungu ali ndi anthu ambiri odabwitsa padziko lonse lapansi. Chimene chachitika muzaka 2,000 zapitazi ndi zakuti anthu amenewa amafunitsitsa kuti asinthe miyoyo yawo ndi kuti akondwetse iye, koma iwo anakhumudwitsidwa. Iwo akhala okanika kupeza kuthekera kwathuthu kwawo ndi kuti amutumikire iye bwino umakhala mtima wawo wonse, koma amalephera kawiri kawiri. Chifukwa chomwe amalepherera ndi choti tamanga molakwika. Ife sitidamange monga mwa kamangidwe, kapangidwe kamene Mulungu watipatsa. Pamene wina ayesera chinthu china, koma achiyesa munjira yolakwikiratu, iye sazapezapo phindu, ngakhale atalimbika motani. Nyumba ya Yesu imangidwa ndi kamangidwe kake, osati yathu. Ndipo kamangidwe kake ndi nyumba ina. "Zana la abambo, la amai, la abale ndi la alongo." Kamangidwe kake ndikakuti "tivomereze machimo athu kwa wina ndi mnzake" ndipo tichiritsidwe. Kamangidwe kake ndi kakuti "tinyamulirane wina ndi mnzake zophinja zathu ndi kuti chinco tikwaniritse lamulo la khristu." Kamangidwe kake ndi kakuti "tikhale amodzi monga iye ndi Atate ali amodzi." Khumbilo la Mulungu kudzakhala nawo pa msonkhano kapena pamwambo, koma khumbiro lake ndi banja lomangidwa pamodzi tsiku lirilonse, lakulukana pamodzi muzigawo zonse zamoyo watsiku ndi tsiku ngati banja.



Yesu wasankha pa Nyumba yake mamangidwe omwe awoneka mofanana dziko lirilonse, osayang'anira ziyankhulo kapena miyambo. Mamangidwe awa ndi amene anthu a Mulungu amapereka miyoyo yawo kukonda ndi kutumikirana wina ndi mnzake tsiku lirilonse, monga banja, pamodzi. Mpingo woona wa yesu, omangidwa munjira yake kuti ukhale olimba, uyenera kukhala banja tsiku lirilonse. Amadyera pamodzi kuchokera kupita khomo lina, amatumikirana ndi kuthandizana wina ndi mnzake munjira zambiri tsiku ndi tsiku.

Amayankhulana za mau a Mulungu wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku kuti awathandize kukhala monga Yesu. Akawona tchimo, apita kukayenda ndi kukayankhula zokhudza tchimolo pamodzi. Sadikira "la Mulungu" kuti akamve wina akulalikira zatchimolo ayi.

Cholinga cha Mulungu (Aefeso 3:10, 1 Petro 2) ndi chakuti ife tonse tiri ansembe a tsiku ndi tsiku ndi akazembe a Mulungu kwa wina ndi mnzake ndi dzake "pamene taima tikhala pansi, ndiponso pamene tiyenda panjira."

Tonsefe tayitanidwa kukhala ansembe a Yesu. Tonse tayitanidwa kuti tikhale ndi mawu a Mulungu ndi kuthandizana wina ndi mnzake. Ichi chitantahuza kuti ngati tiona mzanthu akudzikonda kapena kukwiya, ngati timuona akumwa, kunyada, kuzikweza komwe kumaswa mtima wa Yesu, pamenepo aliyense wa ife atengepo mbali pakuthandizana wina ndi mnzake kuti tisinthe. Izi ndizatsiku ndi tsiku. Zilibe ndi chochita ndi tsiku la Mulungu.

Mpingo woonadi wa Yesu ndiwopangidwa miyala ya moyo, ndipo mamangidwe ake a Nyumbayi ndi banja la tsiku ndi tsiku.

Sichinthu chomwe "timapita kukhala nawo", koma ndi chinthu chomwe tiri tsiku ndi tsiku.

Kodi mukuona mmene zonse izi zalumikizana? Pokha pali ubale wa Tsiku ndi Tsiku ndi pamene ungaziwe ngati wina amakonda kuwala ndi choonadi, ndipo pamenepo ali mwana wa Mulungu. Misonkhano yochepa yam'sabata siyingathandize

wina kudziwa ngati wina ali okonda kuwala ndipo koma ali ofowoka chabe, kapena ngati sakonda kuwala ndipo potero ali osapulumutsidwa. Chikonzero cha Mulungu ndi chuma mu zotengera za chikonzero cha Mulungu ndi unsembe wa okhulupirira. Chikonzero cha Mulungu pa anthu ake ndi "kulimbikitsana wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku." Pamene tikhaladi mzimenezi pamodzi, ubwino umodzi ngwakuti onse a ana a Mulungu amakhwimira khwimira. China mwachotsatira chakuyenda pamodzi ngati momwe Mulungu afunira ndi chakuti ngati wina sakonda kuwala, kenako amaonekera ngati ozilimbambayitsa.

Ngati ali osaweruzika, ngati sasamala za chimene Yesu anena chaokhudza zinthu izi, ngati akwiya ndi kudzitukumula, ndiye kuti aonekera ngati a Khristu oyerekezera. Chimabwera poyera kuti iwo sanapereke moona moyo wawo kwa Yesu chifukwa chilungamo chake ndi chakuti wina sangakhale ndi mzimu oyera ndikupanda kukonda kuwala (Yoh 3, 1 Yohan 1, 3).

Ngati timanga munjira iyi—kusintha kuzikonda kwithu, kapena miyoyo ya ulesi, kuphunzira moonadi mmene lingakonderane wina ndi mnzake ngati banja tsiku ndi tsiku, kutengepo mbali potumikira ndi kuthandizana wina ndi mnzake ndi mau a Mulungu tsiku lirilonse pamenepo lidzakhala nyumba imene Yesu akhoza kukhalamo ndi kuyikonda. Idzakhala nyumba yamamangidwe abwino imene idzakhala yophweka kwa Yesu ndi ife tonse kukhalamo ndi kuyipanga khomo lathu.

Yesu ananena kuti tikachita monga mwamau ake, namondwe akabwera (ndipo adzabwera), pamenepo nyumbayo idzaima. Idzaima chifukwa yamangidwa pa mwala wa "kuyika mau aku muzichitochito," osati mukuganiza kapena mukuyimba zokhudzana ndi mau ake. Ngati ife tiyimba chabe izi, kupephera zokhudza izi ndi kuyankhula za izi osasintha njira za mmene tikhalira mukumvera mau wina ndi mnzake, pamenepo namondwe akabwera, ngakhale nyumba itakongola nzotani, idzasalazidwa ndi kuwonongedwa. Ichi ndi chimene Yesu adalonjeza mu Mateyu 7. Tsono, tsimikizani mukumanga njira yake ndipo PANGANI kanthu pazachoonadi chake. Mverani choonadicho ndipo pamenepo namondwe sadzakupwetekani inu ayi.

Munjira yomweyo mbalame yochepa kapena kalulu wang'ono abisala kunsi kwa thanthwe pamene namondwe abwera, inunso makhoza kubisala kunsi, kunthunzi wa mapiko a Yesu ngati mumanga munjira yomwe iye akuyitanirani inu kuti mumangire. Namondwe agwedeza mitengo ndi kusuntha zinthu zolemera. Zinthu ziombana ndipo mphezi ziomba. Koma ngati inu mumanga monga mwa njira ya Yesi ndi kutembenuzira nkhope zanu kwa iye namondwe akabwera, mudzakhala inu otetezedwa mu munthunzi wa mapiko ake.

Namondwe wamphamvu adzadutsa ndipo dzuwa lidzawala. Mbalame zidzayambanso kuyimba ndipo moyo udzakhalanso watsopano. Idzakhala nyumba yolimba kwambiri ya mamangidwe abwino. Pamene namondwe abwera naomba pa nyumbayi, iyo idzaima chifukwa ili ndi katundu omangira wabwino yekha, ndinso chifukwa ili ndi mamangidwe abwino. Padzakhala kuonongeka kochepa pa nyumbayi ndipo tonse tidzakhala otetezedwa. Monga mmene Atate adanenetsa chindunji za katundu ndi mamangidwe amene Nowa amayenera kugwiritsa ntchito pomanga chombo. Chonchonso Yesu ali ndi kakonzedwe pa katundu ndi mamangidwe a Nyumba yake.

Ndipo kakonzedwe kake, sikapangano latsopano munthu oyera kuyankhula kwa gulku la anthu omwe siwolumikizana "oyima pamfundo yokhala nawo mumisonkhano yotere." Pano TSOPANO ndi mazana a amai, abambo, abale, alongo"—akulukidwa mwakuya m'chikondi "kuchokera ku ung'ono kufikira ku ukulu" waubale wa okonda kuwala.

Uwu ndiye uthenga wabwino wa Ufumu wa Yesu. Iye adati, "Atate anga ali ndi kulimbika pa nyumba yomwe ikumangidwa." Atate akukhumbira koposa kuti timange nyumba yake mnjira yake. Mumayiko ndi mzinda yambiri, nyumba yomangidwa munjira imene Yesu afuna ndiyochepetsetsa. Pafupi—fupi mu

mpingo uliwonse ndi dziko lirilonse muli anthu amene amabwera pamodzi mwa mwambo ndi khalidwe ndipo kenako kupita njira zosiyana, kukhala moyo wawo mmene chiwakondweretsera iwo eni. Mwina amachimwa mwaufulu ndi dala kapena satero konse. Komabe sinyumba ayi chifukwa sakhala ngati banja, tsiku ndi tsiku, pamodzi.

Ndi pamene miyala yonse ikakamirana pamodzi pokha, momatidwa ndi chikondi cha zichitochito ndi ndi kumangidwa ndi mamangidwe a Mulungu, pamene amasanduka malo amene iye akhonza kuwatcha nyumba. Ngakhale uli mwala wamoyo wabwino ndikuyesa kukhala moyo wachiyero, ndi iwebe mwala umodzi. Ngati utenga mwala umenewo nauyika panthaka, sudzakhalabe nyumba ya Yesu. Iye safuna miyala yapayokha yokhala munda chabe ayi. Ife tiyenera tidzipange tokha, ngakhalenso kuzikakamiza tokha, kukakamirana pamodzi ndi miyala ina. Tsiku lirilonse tiyenera kudzilamula tokha kukakamirana pamodzi ndi miyala ina, mumamangidwe a Mulungu a Nyumba --------------------- pamene "tiyimirira, tikhala pansi, pamene tiyenda mumseu" pamodzi. Kuchaya Malaya pamodzi, ndi kupita kumsika pamodzi. Pamene tigwira ntchito mminda, tiumba njerwa, tidula nkhuni, tikonza chakudyatiyeni tichite ichi pamodzi kuti ife tikhale banja limodzi mmalo mwa anthu ambiri kapena mabanja ambiri. Ndi muzochitika "zazing'ona" izi zamoyo wa tsiku ndi tsiku pamene tingalimbitse ndi kulumikidza chikhulupiriro, chiyembekezo ndi chikondi chathu pamodzi. Zochita izi zatsiku ndi tsiku, zokhalidwa pamodzi ngati Banja, ziri "mazenera a moyo" amene amalora ife kusambitsana wina ndi mnzake mmadzi a Mau, koposa.

Cha "kukhala nawo" mu miyambo yachipembezo ndi mmayimbidwe ndi mmauthenga a munthu oyera. Yesu sakumanga chilichose koma mpingo.

Yesu adanena kuti ngati mumveradi funiro langa, mudzakhala ndi mazana a atate, amai, abale ndi alongo—osati anzathu ayi, koma zana la abale a m'banja okondana kwambiri. Ichi ndicho



chifunira cha Mulungu. Izi ndizo ziphunzitso za Yesu Khristu—kuti amanga nyumba yake ndi katundu omangira wabwino. Katundu oyipa Sali olandilidwa ngati safuna kusintha pakumva mau a Yesu.

## Kumanga Kuti Ikhale Ya Mphamvu,

### *Kulimbika Mtima kuti Tisinthe*

Pakatha zaka khumi zokhala a Khristu, anthu ambiri amuzipembedzo zowongoleredwa ndi *Akulu a mpingo* zamaziko ongokhala nawo pakupembedza sakhala wolimba kuposa mmene adaliri mzaka zawo zoyamba. Ichi sichabwino ayi. Ngati mwana wathu wachaka chimodzi akula kufika zaka khumi koma ali opanda mphanvu kapena nzeru koposa mmene adaliri ali ndi chaka chimodzi, ichi chingakhale chokhumudwitsa. Ngati uli ndi mwana wa zaka khumi mubanja mwanu amene adali wofooka ngati mwana wachaka chimodzi—monga tate kapena mai, ichi chikhonza kuswa mtima wanu, kodi sichingatero?

Kodi muganizapo bwanji za Atate wathu a kumwamba m'mene amamvera pamene anthu ake onse ayenera kukhala amphamvu ndi nzeru ndi "ozadzidwa ndi Mzimu Oyera ndi ozadzidwa ndi nzeru," "ndinso oyenera kukhala aphunzitsi panthawi ngati ino" "osati makanda ayi," ogwira ntchito ya Mulungu koma ambiri mw aife sitili amphamvu koposa makanda a chaka chimodzi? Izi ndi zoona padziko lapansi, ndipo zimaswa mtima wa Mulungu. Ife sitingayimbe nyimbo zambiri kapena "kulalika" maulaliki ambiri kuti tisinthe ichi, chifukwa ife sitimanga munjira ya Mulungu mu Nyumba yake ya Mulungu.

Mulungu ali ndi mamangidwe a Nyumba yake akuti timangire kuti ntchimo likhonza kuwomboledwa ndi kuphwanyika. Njira ya Mulungu "yomangira mpingo" imaloreza ubale kuti uchiritsidwe ndiponso tchimo ndi zifooka zichotsedwe. Uwu ndiwo mtima wa Mulungu kwa anthu ake kuzungulira pa dziko lonse. Ife tifuna tikuwuzeni inu m'mene anthu abwino angafikire pamphamvu zakuthekera tsopano.

Ife tikhonza kulola mphatso za m'thupi la Khristu kumangidwa pamodzi kukhala mokhala mwa Mulungu mozazidwa ndi ulemerero wa Mulungu. Pali njira imene Mulungu afuna ife kuti timangire kuti tithe kuwona mphamvu ya machimo ikuphwanyidwa mumoyo weniweni ndiponso ife kusiya kukhala akapolo kuzofooka zathu zonse. Chikonzero cha Mulungu ndi kumanga maubale, osati kukhala ndi mavuto ntahwi zonse. Mulungu ali ndi njira yodabwitsa yomangira nyumba yake ndi anthu odabwitsa.

Mpaka pano, chipembezo mudzikoli chamanga Nyumba ya Mulungu molakwikwa, ndi anthu ngati mabwana ndiponso anthu oyera ndi "kukhala nawo" m'misonkhano ngati matathauziro awo "a'mpingo." Ife sitinadziwe m'mene tingamangire, koma tsopano tiyenera kuphunzira m'mene tingamangire. Mulungu adati tikhale "osamalitsa kwambiri m'mamangidwe." Pali choonadi chapadera chomwe kwanthawi zonse chakhala chili m'Baibulo chomwe chidzasintha moyo wanu ndiponso kusintha njira yomwe Mpingo umaonetseredwa, kuti timkweze m'mwambamwamba Fumu yathu Yesu ndi kuona kuti loto lake lakwaniritsidwa.

Mulungu akufuna kumanga Nyumba yake kuti ife tonse tikhale amphamvu pamodzi. Iye akufuna kumanga Nyumba yake kuti zipata zandende zisadzaipyole. Iye akufuna kumanga Nyumba yake kuti maubale achilitsidwe. Iye akufuna kumanga nyumba yake kuti iye amasuke kuchiza matupi athu, malingaliro ndi miyoyo yathu. Iye akufuna kumanga Nyumba yake kuti ikhale ya mphamvu ndinso nzeru, ndikuti uthenga wabwino wa Yesu upite patali, mwamphamvu kuposa kale.

Kodi inu muli nako kulimbika kuti mumve zinthu izi? Kodi mumvera mau a Mulungu pamene mukumva zinthu izi? Kodi inu musintha miyoyo yanu posawerengera mtengo wake? Ngati muli nako kulimba mtima kuti mumverandipo muzipereka chonde werenganibe.





# YESU:
# *MTSOGOLERI NDI MUTU*

## Utsogoleri wa Yesu
### *Pa Anthu Ake Onse*

Chikhristu chonama kwazaka zambiri chakakhira anthu pansi. Chatenga anthu ochepa ndi kuwakweza pamwamba kuwapanga ena mwa "atsogoleri" olemera ndi otchuka ndi amphamvu kwinaku chipondereza ena pansi. Mumaiko a United States, India, Poland, Brazil, Romania ndi onse padziko pano, muli "ziphona" za akhristu ndi akhristu apansi. Izi ndi zolakwika kwambiri. Yesu adati kw aophunzira ake mu Mateyu 23, "Musatche munthu phunzitsi, tate, mtsogoleri, mbuye, 'rabbi', m'busa pakuti muli abale ndi tate wanu m'modzi! Palibe 'ziphona' mu chikhristu choona kupatula Yesu yekha. Pasakhale mabwana amene amayendetsa ndi kuwongolera maganizo, ndalama, ndiponso anthu—kupatula Yesu kuzera mu Anthu ake pamodzi mwa Mzimu Wake.

Baibulo linena mu Aefeso 4 kuti pamene Yesu adapita kumwamba ndi kutumiza Mzimu Wake, Adatenga mbali za iye yekha ndikuzimwaza pa thupi la Khristu, mpingo. Yesu adatenga

mphatso zonse zomwe ali nazo (ndipo Yesu adali ndi mphatso zambiri, sichoncho?), ndipo anazipereka kwa anthu ake monga thunthu. Sanatenga mphatso zomwe ali nazo ndikuziyika pa 'abusa' kapena pa m'modzi "munthu wa Mulungu". Malembo anena adatenga mphatso zake zonse ndikuzipereka kwa thupi lonse Baibulo linena kuti Mzimu unayikidwa ndi kuperekedwa ngati mphatso, monga m'mene mzimu ufunira, pampingo wonse. Ngati uli nkhristu oona, ngati mwatayadi moyo wako chifukwa cha Yesu. Pamene Mzimu Woyera ukupatsa iwe mphatso yapadera.

Ndipo, mphatsoyako ndi mbali ya Yesu. Pali mitundu yambiri ya mphatso zomwe zidalembedwa m'Baibulo. Mzimu Woyera, mwachitsanzo, umapereka chifundo ngati mphatso. Mphatso ya chifundo ndi mbali ya Yesu imene iye anapeleka kwa ena. Icho ndi mphatso ta uzimu. Tonse ife tiyenera kukhala ndi chifundo, sichoncho? Koma pali chifundo chopambana chimene chili mphatso ya Mzimu Woyera. Ndipo pakuti ulamuliro onse ndi wa Yesu ndi mphatso zonse zimene zili mwa ife ndi mbali yake ya Yesu, ndiye lizipereke ku mphatso zonse zili mwa wina aliyense mwa ife chifukwa ndi Yesu adaikanso.

Munjira iyi, utsogoleri uli mwa anthu onse a Mulungu. Baibulo lititcha ife ufumu wa ansembe. Baibulo silititcha ife kuti ufumu okhala ndi ansembe, koma ufumu wa ansembe. Palibe gulu lapadera ngati a Levi aku chipangano chakale. Mu pangano la tsopano, tonse anthu a Mulungu tikuyenera kukhala ansembe kwa wina ndi mnzake. Funiro la Mulungu siloti munthu m'modzi oyera wapadera ndi amene angalalikire ayi. Baibulo linena kuti Yesu anakwera kumwamba ndi po anapereka mphatso kwa anthu ake onse. Iye adapanga ufumu wa ansembe. Iye adayika gawo lake mwa wina aliyense wa anthu ake amene ali otembenuka moona, ana ndi akulu omwe. Ichi nchifukwa chake timafuna mphatso zawina ndi m'nzake. Ife timafuna mphatso zonse za Yesu! Pali mazana a mphatso chifukwa ZONSE za Yesu zinathiridwa pa Banja Lake. Ichi ndichifukwa Yesu adati tonse tili abale pakati pa abale. Ife sitifuna munthi m'modzi ndi mphatso imodzi kuyimilira kutsogolo kwathu. Ife tisavomereze ichi ayi. Onse ake, otembenuka moona ndi okhala moyo opatulitsidwa wa



tsiku ndi tsiku pa wina ndi mnzake (Aheberi 3:12–14)—Onse ndi ansembe!

Palibe ulamuliro wina wake umene uli mwa "munthu wa Mulungu" m'modzi ndi ena onse kungokhala ndi kuwonerera. Chifukwa chanjira imene anthu amangira mpingo m'zaka zoposa 1800 zapitazo, ife tachila monga ngati pali mphatso imodzi yokha basi—mphatso ya "ubusa". ("kapena mwina wina aliyense ali ololedwa kukhala ndi "mphatso yapadera ndalama"). Koma ubusa ndi mphatso imodzi yokha! Ngati ife timanga molakwika, ife tonse tiluza ngati munthu m'modzi akankhidwira patsogolo kukhala "mbusa" ndipo ena onse azingokhala ndikumamvesela nthawi zonse, ndiye kuti palibe adzagawana nawo gawo la mphatso yawo. Iwo amangotorapo mphatso ya "abusa" ichi ndi chinthu chaching'ono komanso chachinyengo. Ngati ife tifuna kuwona ukulu wa Mulungu, ndipo ngati tifuna kuti tione miyoyo yathu ikusintha ndiponso miyoyo ya ana athu ikusintha, tikufunika ZONSE za Yesu. Mphatso zomwe onse a alongo ndi abale ali nazo ndi gawo la Yesu. Ngakhale ana lai ndi mphatso zomwe ndi gawo la yesu. Ife tonse tikufuna zonse za mphatso pa miyoyo yathu. Ife tonse ndife abale. Mtima wa Mulungu ndi oti mphatso zomwe uli nazo upatse ine ndipo zomwe ndili nazo ine ndipatse iwe. Ife tisakhalire pambali chabe ya mphatso za Yesu. Amen?

Kodi mwawona chomwe tikufunikira kulimbika mtima? Zinthu ziyenera kusintha! Simungapitilire kuchita zomwe mukuchita. Muyenera kusankha kugwiritsa ntchito mphatso yanu kwambiri ndiponso kulandira ena kuti nawonso ateronso. Mupanga chisankho kukhala omvera ndi olimbika mtima. Ngati inu mupitiliza kukhala pampando wanu kapena pansi nthawi zonse ndipo osagwiritsa ntchito mphatso yanu kwambiri ngati m'mene muliri, mphatso yanu idzapitilira kulowa pansi. "Iye amene wakhal akupasidwa chikhulupiriro kapena mphatso ayenera kuonetsa kukhulupirika." Kodi mukukumbuka za munthu yemwe adakwirira talente yake? Yesu adati, "Iwe oyipa, watchito wa ulesi." Icho ndi chomwe yesu anena kwa ife pamene siltipanga chomwe kuyenera kupanga. Ngati ine sindigwiritsa ntchito mphatso yanga

kapena ngati simugwiritsa ntchito mphatso yanu, ife tili "oyipa ndi a ulesi".

Bwanji ngati inuyo mutakhala othamanga wa Olympic, mwagona pa vedi ndipo wina watenga zigwe ndikukumangani? Ngakhale inu mutakhala opambana, ngati munamangidwa pa bedi minofu yanu ikakulungala ndipo mukadafa. Mphamvu zanu zonse zikadatha chifukwa mwamangidwa pa bedipo kwa miyezi ndi zaka. Kodi inu mukuwona miyambo ya anthu abale ndi kulanda Mau a Mulungu? Njira yomwe tinamangira m'zaka zoposa 1500 zapitazo mu nyumba ya Mulungu zamangirira anthu a Mulungu ambiri pa bedi!

Iwo akhala asakutha kuzuka kapena kuthamanga ndi kukwaniritsa chowinda chawo chifukwa anthu amanga molakwika, mosatsatira Mau a Mulungu. Ngati ife timanga mpingo munjira yomwe ikweza munthu ndi tizima mphatso za ena, ndife ophwanya malamulo (zigawenga) ku khoti la kumwamba chifukwa cha kuwonongeka komwe kuchitike chifukwa cha "chotupitsa chochepa muzonse" ndi mphatso zosagwiritsidwa ntchito.

Sichifukwa choti anthu ndi "oyipa" kuti tamanga molakwika. Kwambiri ndichifukwa choti sitimadziwa kamangidwe ka Nyumba ya Mulungu mwa mapangidwe ake kwa zaka 1800, dziko la a khristu asokoneza zokhudzana ndikuti khristu ndu uti,…mtsogoleri ndi ndani… Kodi moyo watsiku ndi tsiku uyenera ukhale bwanji… Ndipo kodi misonkhano iyenera kuoneka bwanji. Atate athu afuna kubwezeretsa zinthu izi kwa ife pamoyo wathu tsopano. Monga m'mene Mau a Mulungu adanyalanyazilidwa munthawi ya masiku a mfumu Yoseya, ndipo chilungamo chinapezeka.

Chokwiriridwa mu zofuna za ufumu wa anthu ndi miyambo yao, tsopano chilungamo cha Mulungu, chomwe chanyalanyazidwa kwanthawi yayitali (koma nthawi zonse chilli mu Baibulo), chikhonza kumasura anthu. Mulungu asintha moyo wanu modabwitsa ndiponso kusintha ena okuzungulirani mosatila mwake.Izi ndi choonadi chopambana ndi champhamvu. Kaya ndi ochepa kapena ambiri mumzinda kapena m'mudzi.



Mulungu sali oletsedwa kupulumutsa kudzera ku ochepa kapena ambiri monga Yonatani mnzake wa Davide adanena. "iye yemwe wakhulupilidwa akuyenera kuonetsa kukhulupirika" Ife tiyenera kukhala olimbika mtima kupanga china chokhudza choonadi chomwe tinanyozera kapena osamvera kumbuyoku.

## Utsogoleri wa Yesu

### *Samuel ndi Sauli*

M'maiko ambiri padziko lapansi pano, tapanga kulakwitsa kwakukulu kukhudzana ndi utsogoleri pampingo. M'malo ambiri munthu amene amaphunzira Baibulo ku seminare kapena kusukulu ya Baibulo, kapena munthu odziwa zamalonda kapena kuyankhula, amapatsidwa utsogoleri kapena "ubusa" Taona ku India ndi maiko ena, nthawi zambiri, kuti munthu ali ndi njinga amenenso angawerenge amasankhidwa kukhala mtsogoleri. Iyi sinjira ya Mulungu! Utsogoleri wa Mulungu sayendera amene angawerenge, kapena amene adziwa kwambiri kapena amene ali ndi chuma kapena maphunziro, mankhwala kapena kuoneka bwino ndiponso njinga.

Ndilongosolepo pamitundu iwiri yautsogoleri yosiyana wina ndi mtsogoleri kuchokera mumtima, kuchokera paubale ndi Mulungu. Wina ndi mtsogoleri wa mpando umene ukhala ndi dzina ndipo ukhonza kutchedwa "wapampando," bwana. Yesu adanena kuti utsogoleri wampando siuyenera. Atsogoleri a Mpingo ndi amene akuyenda chifupi ndi Mulungu LERO. Ngati m'bale kapena mlongo sayenda chifupi ndi Mulungu lero, iye sangayesedwenso mtsogoleri. Ngati munthu sabata yatha mwina sadali chifupi ndi Mulungu koma walapa machimo ake m'moyo wake ndipo tsopano akhonza kumva mau a Mulungu, ali mwa mtsogoleri sabata ino kuposa sabata yatha. "kukhala mtsogoleri" kuchokera paubale ndi Mulungu ndi anthu a Mulungu siwuchokera pa mpando kapena dzina ayi.

Tiri ndi atsogoleri ambiri mumzinda umene ndimakhala, koma tilibe "amipando" Mtsogoleri wasabata ino akhonza osakhala

mtsogoleri sabata yinayo. Yesu adanena kuti ulamuliro onse wa pansi ndi kumwamba ndi wa iye. Ichi ndi choona. Tsopano, ngati tingamumvere Yesu, amene ali ndi ulamuliro momwemonso ndi m'mene munthu ali ndi ulamuliro pokhapokha ngati akhonza kumumvera Yesu, Ichi ndiye zonse. "ulamuliro onse wa padziko ndi kumwamba" uli ndi Yesu, iye adanena. Munthu amene samdziwa kapena kumumvera Yesu ali ngati "mukuyerekezera" chabe. Munthu otere akhonza kufuna kuti azimumvera monga m'mene thupi livomerezera, ngati ali ndi "mpando" koma iye ali "mtsogoleri" pokhapokha ngati adziwa, akonda, ndipo amvera Mutu, Yesu.

Pali chitsanzo m'Baibulo cha mautsogoleri awiri amenewa. Samueli ndi Sauli onse adali atsogoleri

a anthu a Mulungu, Israeli. Samueli adali munthu wa Mulungu amene adali ndi chikoka mu fuko chifukwa amadziwa Mulungu. Samueli adali ndi zothekera zambiri zaufumu ku Israeli—koma Samueli sadali mfumu! Komabe, Sauli adatchedwa mfumu. Israeli imafuna kukhala ndi mfumu—amafuna kukhala ndi munthu modzi kukhala bwana. Amafuna wina kuti alowe mmalo mwa Samueli ndipo amafuna "mfumu" monga mafuko onse owazungulira. Munjira ina utsogoleriwu ukhonza kuwoneka mofanafana, koma Samueli alibe "mpando" wa ulamuliro. Samueli amagwira ntchito kuchokera paubale wake ndi Mulungu, ndipo Sauli amagwira ntchito kuchokera pampando wake. Samueli adalibe ofesi, mlembi kapena malipiro (salare). Iye sadali muudindo wa mpando ngati mfumu. Samueli adali chabe munthu wa Mulungu amene amalemekezedwa ngati mfumu koma adalibe mpando kapena ofesi. Iye sadali mfumu iye sadali "mbusa". Iye amangokonda Mulungu ndi mtima wake onse.

Ndipo chifukwa choti amamvera Mulungu, adali ndi chikoka. ***Adalibe mpando adali ndi chikoka.*** Ngati munthu moonadi adziwa Mulungu, adzathandiza anthu a Mulungu. Ngati wayitanidwa ndi Mulungu, adzakhala akuthandizila anthu. Ndibwerezanso: Munthu wa Mulungu oona alibe mpando… ali ndi chikoka. Yobu 29, ikulongosola za munthu olemekezedwa



ndi Mulungu ndi anthu, ndi woopedwa ndi odedwa ndi satana. Munthu otere safuna ofesi kapena dzina kapena malipiro. Ngati muli ngati Yesu, simudzafuna "mphamvu."

Monga mwachitsanzo, ngati ndili m'misili, ndi mapanga zinthu ndi matabwa. Ndimapanga mpando, tebulo kapena chitseko kuchokera ku matabwa. Ngati ndili omanga, ndiye kuti ndimanga zinthu ndi njerwa. Chinachake chomwe ndipanga kuchokera ku njerwa ndi umboni oti ndine omanga. China chake dzomwe ndipanga kuchokera kuthabwa ndi umboni oti ndine m'misili. Tsopano, mu Baibulo mau awa "mbusa" (kutathauza kolakwika) koma atanthauzira kuti mphatso ya ubusa wa nkhosa, ogwira ntchito tsiku ndi tsiku pakati pa anthu a Mulungu moyendezana (mwapambali) pa mphatso zina—osati bwana kapena "olankhula wamkulu" pamsonkhano. Kodi umboni uli pati kuti ndine Mbusa weniweni? Umboni ndi wakuti ine ndimakonda anthu a Mulungu! Ndimawathandiza iwo usana ndi utsiku. Sindifuna dzina, sindifuna kukhala bwana. Ndimangokonda anthu ndi mphatso yomwe ndili nayoyi, ndikuwathandiza. Umboni waumusili ndi mpando omwe ndapanga umboni woti ndine **Mbusa weniweni** ndi woti ndimadyetsa anthu a Mulungu tsiku ndi tsiku, ndipo ali chifupi ndi Yesu chifukwa cha ine. Ngati ndiwona kuti m'modzi mwa anthu a Mulungu ali ndi njala, chimandiswa mtima. Ngati ndiwona kuti m'modzi mwa anthu a Mulungu ali muvuto kapena muzoopsa, mtima waubusa mkati mwanga uthamangira iwo kukawateteza. Uwu ndiye umboni oti ndine odzodzedwa wa Mulungu kukhala m'busa. Sindifuna mayina opatsidwa. Sindifuna chitupa chopachika pakhomo ndi chochokera ku Sukulu ya Baibulo. Ndifunitsa mtima okonda ndi kuchita ntchito ya Mulungu, ndipo kenako ndizabala zipatso zauzimu mumbali iliyonse yomwe iye azandipatsa ine.

Tsono, ndinu m'misili? Ndiye pangani mpando. Muli ndi mphatso ya ubusa. Ndiye kondani anthu—adyetseni, atetezeni ndipo athandizeni. Ichi ndi choona pa mphatso iliyonse! Umboni wa mphatso iliyonse uli mudzipatso zimene umabereka.

Zotsutsana za zonsezi ndi zoonanso ndithu. Ndifundo yodabwitsa kuti amafano mu sayansi ndi mankhwala ndi

malonda amalamula kuti amene ali ndi maganizo ndi mtsutso ndi odzitcha okha "akatswiri" ali ndi china choti awonetse, zipatso mumiyoyo yawo, awonekera kuti ali dni ufulu wolamulira, kuphunzitsa kapena kutsutsa ena. Mudziko lachipembedzo, modabwitsa, ali ndi ungiro ochepa kuposa ngakhale zimene amafano amaonetsera. Muchipembedzo, ngakhale, anthu ali akhungu ndi wozunguzidwa kwambiri.

Mtsutso, ukatswiri, zigamulo, ndi ngakhale ubale ndi zonyoza zimayenda mophweka kuchokera kwa iwo azipatso zoyipa miyoyo yawo, m'mabanja ndi m'mabwalo awo. Zodabwitsa, koma zoona ngati inu muona chipembedzo chamunthu mosamalitsa ndi moona. Munthu amene amapanga zinthu zotere ngati bodza kapena m'nyozo kapena kukhala ngati katswiri pa njiniaring'I, zamakhwala kapena malonda akhonza kusonkhanitsa pamodzi gulu lomvera mpphweka anthu akuopa, m'mene akhonza kunderedwa pansi, kapena kuyamikiridwa mpusitsa ku—kuzipereka ku makina osabereka zipatso ndi "akatswiri" zonga zamisala koma ndi zoona. Zimachitika kunthawi zonse, chifukwa umu ndi m'mene maufumu a vuto amasungira nambala yao. Mantha ndi kuyimikira kopusitsa, mjedo, m'nyozo kapena kuyenderedwa pansi. Nchifukwa chake ziri zosadabwitsa kuti Yesu sanapange bwino mu chipembedzo chovomerezedwa kudziko lapansi cha munthawi yake. Koma, likhonza kuphunzira kwa iye ndi kusunga malembo, ndi kuyang'ana zipatso, osati kumvera—kunena kwa mfundo ndi mabanjeti, ndiponso kunena kufuna kwa yenkha kwa munthu kuti ateteze.

(Pamenepo mwatengapo mfundo. :)

## Utsogoleli Wa Yesu
### *Mu Msonkhano*

China chimene tiyenela kulimba mtima kusintha ndikukhala ndi msonkhano monga baibulo limanane mu 1 Akorinto 14: "Pamene mubwela pamodzi, abale mpingo onse uli pamodzi, zilizonse zichitike mukumanga tonse pamodzi aliyense ali ndi



chimangililo, nyimbo, bvumbulutso" ngati tidzakhala motero, potero osakhulupilira adzagwetsa nkhope nanena kuti, "Mulungu ali nanu".

Palibe bwana wina pambali pa Yesu "Musamutche wina mtsogoleri, Ambuye mphunzitsi, kapena mbusa. Ndinu nonse abale" muli ndi Yesu ndipo ndiofanana mwa inu nonse. Inde pali kusiyana kwa makulidwe, ndipo mphatso zina ndi "zoonekera" ndipo zina ai kapena zochepa kuonekera pa malongosodwe. Koma zonse zilipo ndipo zili ndi mwai. Nthawi zina timafuna chifundo cha Yesu ndipo nthawi zina timafuna kuphunzira kwa Yesu. Nthawi zina nyimbo kwa Yesu. Ndipo nthawi zina timafuna kuthandizidwa kwa Yesu pothana ndi zobvuta. Koma zonse ndi zofanana mwa Yesu chonde werengani 1 Akorinto 14:26–40. Palibe amene ali olamula, koma Yesu yekha. Timasonkhana pozindikila kukhalira pamodzi, mchikondi ndi ntchito zabwino" (Aheberi 10:24–26) Tiyenela kuganiza za pemphelo mmene tingathandizilane wina ndi mnzake pamene tili pamodzi, ndipo yense wa ife ali ndi udindo pa mau a Mulungu ndi chikondi chake. Popanda wina opambana" oikidwa kuchita kalikonse kupatula kumvela ndi kubvomereza kwa Mulungu monga wina aliyense ngati wina abweletsa chiphunzitso kuchokera kwa Yesu ndipo ena chimangiliro kapena nyimbo, kapena bvumbulutso, ngati mbale, mlongo agawa kanthu kamene Yesu waunetsela ndipo bvumbulutso lidza kwa wina okhalapo ndipo olankhulawo akhale pansi—ngati timvela malangizo a Mulungu, osati mwambo ya anthu chabe. Baibulo limanena nthawi zonse, ngati bvumbulutso lidza kwa wina okhalapo. "OYAMBA AYENELA KUKHALA PANSI" ndi zimene amanena mu 1 Akorinto 14.

Izi sizabwino kwa iwo amene amafuna kukhala otchuka ndi okonda kukhala akulu utsogolera ndipo owoneka ngati auzimu ndikumatenga ndalama za abale woyera mtima ife tatengela katundu olemela mu miambo kuchokera kwa Akatolika ndiponso kwa ma potesistant, ndi mpingo ya chipembedzo ndi ya makolo athu, akale. Mbusa kapena otsogolera zochitika amakhala patsogolo pathu kulankhula ndi ang'ono, anthu osadziwa

kanthu ndipo ena onse amakhala ndi kumvetsela. Izi ndi zinthu zimene maphunzitso ake, Yesu anati, amadana nazo, ndimene zimalamulila anthu mokakamiza, koma Mulungu akuti zonsezi zisinthe, pa ubwino wa iye ndi ife.


Mwachoncho, ine ndikuganiza motele kwa inu kuti ngati tifuna kulemekeza mphatso imene ili mwa ife, ndikubweletsa mphatso zonse zili mwa anthu a Mulungu ndiye pafunika kusintha zinthu zambiri. Zopusa mmamvekedwe, mwa zina ndi mmene timakhalila mu msonkhano pamene takumana pamodzi. Pamene Yesu anali pano, iye, anthu amazungulila—Awa ndiwo anali abale, alongo Mariko 3. kukhala mozungulila iye! Zizoyenela kukhala motelo, pamene tili pamodzi ndi kumvetsera kwa iye osati munthu wamba okhala ndi mphatso zochepa ai? Zimenezi zosabvuta kwa inu zingaonekeso ngati zosafunikila, koma ndinenetsa kwa inu kuti mau oti "Pupeti" ndi "thupi" amanenedwanso choncho mu chi french.

Pamene tikhala tonse kuona ku tsogolo, zimaonetsela munthu m'modzi yekha. Sitikhalanso ofanana ai ndimakhala kapolo wa iye amene wakhala kutsogolo kwanga monga Ambuye, kapena undidziwitsa za pamseu, msilikali kapena mu kalasi kapenanso mumapemphelo. Pamene timaika mipando mmizire mmalo mwa chokala mozungulila Yesu, zimakhala ngati kuonekela kwa munthu mmodzi yekha ali owonekera izi ndi zoipa chifukwa pali mphatso zambiri mwa ife ndipo zili mbali ya Yesu. Ngati tiika anthu onse kuona patsogolo, ndiye tikukweza mphatso imodzi yokha. Kungatheke bwanji munthu modzi wonyada kulora yekha nthawi zonse kukhala patsogolo kapenanso poonekela.

Mu chithunzi chili pansichi, kweni kweni chipembetso mmachitidwe owonetsela mu anthu, ndi "mipingo ya nyumba" alipo munthu wamba amene amakhala otsogolera, mwa iye onse amatsalira. Iye amayamba amamaliza amaphunzitsa kapena kugawa ntchito zina, kuphunzitsa "kupembedza" amalamulira zonse, kuyankha mafunso. Ndi kutsogolera onse Awa simau abaibulo ai 1 Akorinto 14:26 kuchepela monga mofunikila chotupitsa mu mtanda, umadzimitsa mphatso, ndi Yesu amataya



umbuye mmaonetseledwe amenewa. Komanso njira zimenezo mulibe mbaibulo siziyenela kuhala choncho.





Kwa dziko lonse (kudziko lonse) chipembetso, kuphatikiza chikhalidwe cha chikristu) kupondeleza anthu mmachitidwe ndi zokozelathu zochitika sizili mu Baibulo, kapena pamtima wa Mulungu ndi maganizo ake. Yesu adalankhula mwachindunji ndi momveka, nazipatsa maina kotsutsana machitidwe odzadza ndi miambo ndi kuitanidza odzalalikila ndi ozikweza okha pa anthu a Mulungu. Ngakhale atumwi khumi ndi awili aja a mwana wa nkhosa adali abale pakati pa abale pakati pa oyela mtima osati oposa ena, monga mw aYesu mwini. Mulungu amakonda utsogoleri wa Samueli pakati pakati pa moyo wa abale osati udindo kapena kutchuka, koma chikondi ndi mphatso monga zifunikila. "Timakana Mulungu" pamene tifuna mtundu wa mtsogoleri wa Sauli, monga mwa chitsimikizo cha Samueli ndi anthu ake mwa choncho uku ndi kuitanidwa kopambana koposa miambo ya anthu zomwe zili zochokera mukuganiza za mmutu mu nthawi zino, koma mpaka titabwelelanso mu njira ya malemba, ndidzapitilabe kukhala ofunda, zotsalira za zotupitsa, monga mmene chikhalidwe cha chipembedzo chimachita.

Pano pali mbali ina tiiganizile. Timakhala nthawi yonse "muza" Yesu "kuchokela Yesu" kumvela ndi kuleza mtima ndi ufulu wa oyela mtima yonse posintha zinthu "kuchokela ndi kudzela mwa iye ndi mwa iye muli kukwanitsa zonse" zomangidwa ndi anthu "odzaonelela" ndi oyela mmodzi chikristu chamizidwa mukusapambana Yesu satha kupeza njira mwa inu, kapena kudzela mwa inu, kapena pamene sasangalala pamene anthu aumiliza anthu ndi zochita zawo" ndi mphamvu yonse yachabe. Kupatsa mantha, kutsatsa popeza mphindu la chuma pazomwe zimachitika mu chipembedzo cha anthu. Zosadabwitsa pamaoneka zimphamvu ndi mau otsulidwa pamene izi zikuchitika kwa ambiri mwa iwo ndi mwala wapangodya umene amisili omanga nyumba anaukana umenewo unakhala mwala wapa ngodya. Amisili ndiwo amene ali ndi zinthu zoonongeka, kapena amaganiza kuti ali ndi zinthu zotaika chifukwa sanathe kukwanilitsa kudalila Yesu safuna isi ali (Mateyu 23 ndi zina zotero) zomanga anthu ndi maudindo a chipembedzo zimene zili ponse ponse lero. Ndizochititsa manyazi ndi kugonjetsedwa chifukwa mpatso zoonongedwa chabe, ndi luwi lake silimvekanso ndipo ndi zoona kuti angokhala kuti uthengawu ndi wabwino, kapena ndi wabaibulo kapena nyimbo ndi yokhudza kudzaonelera kokha, machitidwe owomiliza anthu sichipembedzo chochokera kwa iye.

Ngakhale sitikhala ngati za iye sizingathe kusintha kwa ife kuti mako a kumdima sangapambane" kapena kugonjetsedwa pa moyo wa tsiku ndk tsiku (1 Akorinto 12, Machtidwe 2:42–47, Aheberi 3:12–14) Iye afuna kukhala mutu osati wa mpingo wake osati zochitika za amene asonkhana mdzina lake.

Nanga kotani mphatso zonse ndi zofanana pamalo amodzi? Ngati pali mphatso ya ubusa kukhala mozungulila ndipo wina mphatso ya uphunzitsi akhala pano ndipo ya chifundo kukhala apo. Mphatso ya kuthandiza ikhala pano ndi wina wa mphatso ya kunenela akhala apa. Zonsezi zili ndi zofanana chifukwa zili za Yesu mwini!






Monga tinanena kale, Paulo mu 1 Akorinto 14 limanena pamene "mpingowose" uli pamodzi. Ananena machitidwe a bale oyera mtima onse ali ndi ndi Yesu akhale mkati mwawo. (chapitala 12) amene amakhala pamodzi pansi pa ulamuliro ayenela kupitila kukhala ansembe pamene mpingo ukhala malo amodzi. Onse ali ndi mwayi obvomela kwa Yesu ku utsogoleri, monga ansembe woona, paliponse pamene mpingo uli pamodzi, palibe kuphangila kapena kusankhilatu wankhulu wachipembedzo mwamuna kapena mkazi kulalikila zimene zakonzedwa kale kulalikila kapena nyimbo. Ndipo machitidwe a "pamene bvumbulutso lafika kwa okhalapo, ayenela winayo kukhala pansi "ndilimene limasunga chithunzi chipangano chatsopano cha Yesu" muutsogoleri mu msonkhano mu "ufumu wa Ansembe" ndipo mphatso limatsandulidwa pa thupi la Yesu, Mpingo wake, ungagwire ntchito nthawi yonse yopelekedwa. Pamene bvumbulutso labwela kwa okhalapo, oyambayo ayenela kukhala pansi atelo Ambuye. Palibe malo opwinja wina pazochitika zilizonse, zokonzedwelatu kale makupeka nyimbo, kapena zosangalatsa, kapena muzochitika zilizonse.

Mumpingo umene Yesu amaonekela wa moyo, wochita-chita ndi wamoyo osakhala mbili yakale yoyelekeza imene iyamikilidwa ndi kuphunzitsidwa, apali ufulu. Aliyense amene ali ndi Yesu okhala mkati ndi kuchita-chita monga tsiku ndi tsiku pakatipa abale, ali ndi udindo kupeleka mphatso "mukumangilira thupi lonse" zonse Yesu anapeleka mu thupi lake, mu mphatso zonse—ndipo zifunika mu nthawi ili yonse. Ngati mnyamata atsegula pa zobvuta zake kumalo antchito ake, mphatso ya uphunzitsi, kapena kulimbikitsa, kapena ubusa kapenanso kuthandiza zikumanizana pamodzi monga bvumbulutso wofika kwa wina wa chiwili "ichi ndi :chinthunzi" cha nthawi imene mpingo wonse "ukhala pamodzi" mwa mkwatibwi. Ndipo mu "chinthunzichi" Yesu amaloledwa kukhala mutu wa modzi pa mpingo wake, osakhala mu kachisi omangidwa ndi anthu ai, utsogolezedwa ndi anthu chabe.

Munthu aliyense ukhale ndi Yesu wamoyo amakhala omasuka kuchita ndi kugwiritsidwa ndi Yesu pakubvomela pa zomwe zikuchitikazo. Zimenezo zokha ndiwo "thupi la Yesu" "msomkhano" uyenela kukhala.

Kusefukila kwa zimene zachitika kale mu tsiku lonse mu "nyumba ndi nyumba" pamodzi—mu moyo wa Yesu. Payenda kukhala malo a Yesu kulamulira ndi kutsogozedwa kudzela mwa anthu ndi mphatso NTHAWI ZONSE, mu zinyumba ndipo zotchedwa "kukumana" Anthu adzachepetsa popeleka mphatso "mu nthawiya kutumukila"—mu zonse ndi kuziowonela okha. Musalore zofanizila chabe pamene Yesu akhala mu mphatso ndi anthu ake.

Mu mtima wa "ufumu wa Ansembe" mmene Yesu kweni kweni amaonekela monga mutu wa thupi lake—ndilo phunziro lathu ndipo kukambilana kwathu sikwazibwana ndi zosapezeka mu Baibulo ai. "zamakanda chabe" ndipo aliyense amene "angatenge mbali" ndi kuchotsa umbuli ndi malingaliro kapena kuti aliyense ayenela kulankhula kanthu" ndipo ngati udalankhula mphindi mopitilila zasanu 'sabata yapita" ndiye sikuti udzalankhulanso zotelo lero. Potelo mpingo siwaufulu otelo ai, mpingo wake ndi wa ulamuliro wa Mulungu pamene KUDZOZA ndi MPHATSO ndi









MAGANIZO A LERO amalamula mu ulumikizo mu kudabwitsa ndi wosasintha njila zosakonzelathu. Munthawi (yosankonzeka) munthu mmodzi angabvomeleze Mulungu mokweza mau kwa nthawi yaitali. Koma sikhala "chomwechi" kwa nthawi zonse.

Pali ufulu ndi kumveka ku njila yake 1 Akorinto 14 sungani ndi kuzindikila kuti Paulo ananenanso mu chaputala kuti palinso kuononga kwa anthu amene samvela utsogoleri wa Yesu, kaepna kupeza mwayi kuchokela mu "ufulu" mukuzikonda, kuchitapo, ndi kusowa nzeru. Penanso, kumbukilani kuti mu malembo wonse amu 1 Akorinto 14 kuphatikiza 10 mpaka 13 pamene moyo wa Mulungu ndi oti Anthu akhala "monga mkate umodzi" kuzindikila thupi ndi kukhala pamodzi olumikizana monga dzanja ndi zala ndi mu mfundo mu malembo amenewa amu moyo wa Baibulo mu mpingo 1Akorinto 14 ziyenelanso kutsatilidwa.

Pamene Bvumbulutso lili ndi ukhalapo, ndipo oimililayo akhale pansi, osati “chiwonetselo chabe ai” kapena “munthu oyela” ayendetse zochitika zonse. “Ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawi zonse.” Kuopa, umbombo, mphamvu ndi kuzikonda kwa anthu ochepa sikungathe kuba anthu a Mulungu cholowa chawo Yesu ali ndi Moyo ndi ALANKHULA kuthyola mu “mphatso zake” monga iye afunila monga ife tili thupi lake osakhala mukuchita mu machita-chita pa tsiku lopatulika.

Inde, pangakhale “oyanganila” amene angatumikile mukuthandiza muzochitika. Ndipo, inde, pangakhale nthawi yolalika, kwa anthu osakhulupilira pabwalo monga Paulo adachitila m’malo ena monga linenela bukhu la Machitidwe, koma mosiyana ndi lero ingakhale adatumikila “polalika” padali kukambilana (Mau a chigriki amene adachitika ku Toasi) osati monga zichitikila makono ai, ndipo kulalika kotero kwa anthu osakhulupilira mu Aefeso kapena ku Anthens chisakhale chinthu chosemphana ndi monga m’mene “mpingo wonse udali pamodzi” monga m’mene osakhulupilira angakhalenso pamene Banja la Mulungu likhalila. 1 Akorinto 14: Nthawi imene mpingo wa Yesu uli pamodzi wina ndi mnzake pamalo amodzi ndi zosiyana ndi pamene wina “‘alalikila mu mseu” kwa anthu ochuluka sukulu kucholinga cholalikila kwa anthu osatembenuka za Yesu, Machitidwe 19:8–10 kulankhula mau a Mulungu kwa ‘onse osakhulupila aku Asia. Izi ndi zosiyana pamene mpingo wonse pamodzi, woomboledwa ndi kukhala pamene akomana pamodzi monga mu 1 Akorinto 12-14 kapena Machitidwe 20. Pamene Paulo analankhula (monga mmau achigriki) ndi banja lake mpaka kutuluka kwa dzuwa mu usiku onse.

Yesu amafuna kumanga mpingo umene makomo a ndende sangathe kupambana. Mmenemo ndimo m’mene anthu onse adzaziwa kuti muli akuphunzira anga. Amafuna ife tonse kukhala malo okhalamo iye—tsiku olumikizana, kulumizika ndi kukumana pamodzi ndi “kukhalira monga mmodzi wa chikhulupiriro” ndi chikondi chenicheni cha “Amayi, mbale, mlongo” mukupambana kwa moyo umene Yesu ali ndiye anthu ake onse (kuchokela kukumphuka kwa moyo wa tsiku ndi tsiku mukulumikizika kwenikweni. Machitidwe 2:42–47, 1 Akorinto 12:13) umagwiritsidwa ndi mzimu wa Kristo mu nthawi yopezeka yonse ndizotelotu monga m’mene adali ndi ife mu nthupi pansi pano. Yesu adati, pamene ife sitimiza mzimu wake ndi zomangidwa ndi anthu, maganizo ndi miambo ndi zowonetsela, ndi kukhala moyo wa ife tokha. Iye ali ndi ufulu wozionetsela yekha mu mphatso monga m’mene adali pansi pano mthupi. M’maganizo ake tsopano ndi kudzoza, kaya ndi chokhumba chathu. Pamene bvumbulutso libwela kwa wachiwiri, wina woyamba akhale pansi.

## Utsogoleri wa Yesu Mu Moyo

Talankhula zonsezi ndi zofunikanso kunena kuti palibe zonsezi kukwanila ngati palibe moyo wa tsiku ndi tsiku monga 1 Akorinto 12–13 pokonzekeretsa chaputala 14,” popanda moyo wa tsiku ndi tsiku izi ndi “zoopsya” sitingalankhula za “msonkhano” posiya zofunika kwambiri. Nkhani iyi ndi yayikulu. Uku ndi kupambana ndi kukula kwa moyo mwa Yesu kwa anthu ake mudziko lino, mosalumikizana, moyo wa yekha okhala ndi anthu achipembedzo ndi chofunika zokonzelathu ndi munthu oyera m’modzi yekha umakhala kwenikweni motere kuchokera muzachilendo, kupenya moipa, anthu ochimwa amagwilitsa “ufulu pa mwamba pa zofuna zawo. Moyo weniweni, 1 Akorinto 12–13 ndi choyambilira potikonzetsela mu ufulu wa mu 1 Akorinto 14.

Tiyenela kuphatikiza “zinthizi” zonse zambuyomu panthawi yomwe mtima yonse ali pamodzi monga ansembe achifumu osati ngati wowonelera monga zikhalila (Efeso 3:10) moyo wa tsiku ndi tsiku wa Machitidwe 2:42–47, 1 Akorinto 12, Aheberi 3:12–12, ndi a MAI AMBIRI (chikwi) abale ndi alongo. Yesu adati iyi ndi chikonzero **Ndi moyo wopambana umene adatiitanira anthu ake kukhala pamodzi paliponse osati makonzedwe a “misonkhano”** Afuna kukhala nazo zathu osati, “msonkhano” kapena kugawa nzeru, kapena kuimba chabe mtima wake uli pa munthu hiwanthunthu. Luka 9:23–27, 57–62. “Chipembedzo choona kuyambila wang’ono mpaka wamkulu” kubvala mzimu wake.

Sizongokhala pang'ono mofewa mu msonkhano wokonzedwelatu kapena osakonzedwelatu, ndi kumatiwotsogozedwa ndi Mzimu' osati chifukwa sitidziwilatu zimene tidzachite ndiye kuti titsogozedwa ndi mzimu sinchonho. Sizotelo ai motero monga Jannes ndi Jambles. Zoyelekeza zimaonetsedwa kuchokera za maonekedwe a dziko, kuoneka ngati zoonazo.

Kusiyana kwa chipembedzo chosinthika ndi kukhala mu zenizeni wa woukawo, yesu wamoyo ndi zokokerana. Msonkhano wokonzedwanso mwamakono ndi zochitika, (ndi zoikidwa) kapena mu "nyumba" sindizo zofunika zenizeni poyelekeza ndi mwayi omwe yapatsidwa ndi ife lero.

Iye sanatitanile ife kuzatsopano ndi zosinthika mamangidwe. Watitanila ife ku moyo watsiku ndi tsiku odya pamodzi ku mtengo wa moyo, ndi odzozedwayo! Inde zimenezi zidzasintha "misonkhano" koma ichi ndi chipatso, osati polekezela, osati kungoyamba zatsopano ndi chiphunzitsp chabwino, zochita, msonkhano wa mphamvu, m'mene anthu amakhalira pamodzi mu Baibulo mulibe. Zofafanirapo, kapena chiwelenge lero chatsopano m'mayendedwe ndi zopanda thandizo kumene osati choonadi. (zimene timayenela kupeza, kufuna zimene iye afuna) ndi malo amene Yesu angakhale ndi kuchita Chibvumbulutso 1-2 popanda choletsa monga wamoyo. Mfumu yokwezedwa ndi moyo wokhawo wodzadza (monga Yesu amanenela) chauzimu moyo wa kumwamba, yolimbikitsidwa ndi mawonekedwa wapamwamba, onse pamodzi kuphatikiza choonadi cha mphamvu yosaoneka wa m'mwamba ndi choonadi ndi chikondi ndi moyo Yesu anabweletsa uwu moyo kukudzanza. "Mitsinje wa madzi a moyo" moyo kwa anthu ake kuchokera mu mlengalenga, dziko losaoneka ndi maso a munthu ndi maonekedwe a pansi pano.

Moyo wa Yesu pamodzi siza misonkhano, zimene Yesu anabweletsa ku dziko lapansi ndi uthenga wa Angelo sangakhale osazama ndi moyo osatha ndi zotele ai. Msonkhano umene anthu ambiri amachita nayo ndi umene Yesu anafera. Sinchoncho! Yesu sanabwele kudziko lapansi kubweletsa njila yatsopano



ya msonkhano kapena mpingo kapena bungwe sizili choncho poyelekeza kuti mu Eklesia azindikilitse (Efeso 3:10) iye afuna kuphwanya kuononga ndi kusokoneza mdani—ndi kusintha moyo ku moyo mu chikhalidwe ndi moyo ndi nzeru ndi mphamvu za mwana. Iye akubweletsa ana ambiri ku ulemerero" osati ku chipulumutso chokha. Akumanga MPINGO wake umene makomo andende sangapambane mwa chisomo cha Yesu Kristo ndi ulamuliro wake, tikutenga ana anthu ndi akanzi omwe ndi mabanja ndi oyandikilana nawo kuchokera ku chinsiriro ndi ukapolo wa satana. Miyoyo yasintha watibweletsa ife kumalo atsopano m'mwamba pambali yake. Mphweya watsopano wopuma, maso atsopano woyang'anila, makutu atsopano womvela mtima watsopano wodziwa, ndi chikondi, kusintha uku ndi kwa zonse mu moyo, kuphatikiza "msonkhano"!

Mukaona zimenezi zimatengela kulimba mtima? Mukuona zimenezi zimatengela chikhulupiliro ndi kumvela? Mukaona zimenezi zimene zingasinthe moyo wanu ngati muyamba kukhala mu zimenezi? Simudzaulizidwa kupita pa kama! Ife ndife ansembe achifumu tsiku ndi tsiku. Ndipo msonkhano udzakhala wowonjezerapo. Inde, zochuluka kwambiri zimakhala zochokela mu moyo wa pamodzi ndiye kuti muyenela kukonza nyumba zanu ndi mzinyumba za ena. Kutenga madzi, kapena chakudya, kapena chobvala ku nyumba zawo. Mukaona kuti ali okwiya ndi mwana, aitanileni pambali ndi lankhula nawo kapena kuyenda nawo mukaona kuzikweza mwa iwo, ikani mnkhono wanu pa iwo ndi kuwafunsa kuti osamatero, mukaona kuzikonda mwa moyo wa mbale ikani mkono wanu pa iye ndi kuti choonde "muzamazikondenso" sitingotseka maso anthu mpaka msonkhano wina. Timakhala pakati pa moyo wa wina tsiku lililonse ngati Ansembe pochita ntchito ya Mulungu ndi amai ambiri, abale, alongo" Ili ndi lamulo lochokera kw aMulungu mu Ahebri 3, ndi malemba ena ambili otele.

**Aheberi 3:12–14. "***Tapenyani, abale, kuti kapena ukakhale mwa wina wa inu mtima woipa osakhulupirira, wakulekani ndi Mulungu wamoyo, komatu ndikudandaulilani nokha* ***tsiku ndi tsiku*** *pamene patchedwa lero kuti angaumitsidwe wina*

*wa inu ndi chenjelero la uchimo. Pakuti takhala ife olandilana ndi Kristu ngatitu tigwiritsa chiyambi cha kuitana kwathu kuchigwira kufikira chitsiliziro.*

Tamvani chomwe malembowa anena ichi ndi chochoka kwa Mulungu. Mulungu wa mphamvu akunena kwa inu ndi ine kuti tiyenera, tsiku ndi tsiku, kuchenjezana ndi kuthandizana wina ndi mnzake. Ife tiyenera kukhala kumbali yawina ndi mnzake tsiku lirilonse. Mzimu Oyera unasankha kunena kuti tsiku lirilonse. Siwudanene kuti la Mulungu lirilonse.

Siudanene kuti la Mulungu ndi lachitatu lirilonse. Siudanene kuti mu misonkhano mokha ayi. Udanena kuti khalani pachilungamo mumoyo wa wina ndi mnzake tsiku lirilonse ngati ena ali kupezeka, ndipo inu simukhala nawo chifukwa cha makhalidwe a moyo wanu, kapena kudzitamandira, kapena kudzikonda, kapena chifukwa chachitsankho cha mmene mungakhalire m'moyo wanu, Mulungu akunena kuti inu mudzakhala owuma mtima ndipo opanda kuthekera kwa kumva monga iye amvera. Inu mudzapusitsidwa kuti mukudziwa chowona pamene simudziwa. Icho ndicho malembo anena mwatchutchutchu! Iye sadangoti kuti mupange ichi. Iye adanena kuti ngati simupanga ichi, chidzakupwetekani inu kwambiri. Ngati ine ndilibe abale ondiyakhula ine tsiku ndi tsiku zokhudza moyo wanga *tsiku ndi tsiku* ndidzakhala ndi kuuma mtima. Ine ndidzakhala ndi kupusitsidwa. Inu mukhodza kunena "koma ndimawerenga Baibulo tsiku lirilonse!" "Koma ndimapemphera tsiku lirilonse!" "Mkazi wanga ndi m'khristu ndipo ndimamuona tsiku lirilonse!" Icho sidzomwe Mulungu adanena. Inu mukhonza kuwerenga Baibulo ndi kupemphera tsiku lirilonse. Koma ngati inu simufuna kukhalilana wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku, uzakhala **mtima wanu** ukuumira, umirabe ndipo inu mukupisitsiwa pusitsidwabe. Mulungu akunena ichi ku Ahebri 3:12–14. Kodi mumakhulupirira Baibulo? Kodi mumakhulupirira Mulungu?

Kodi adalemba Baibulo ndi ndani? Mulungu, Mulungu adanena kuti tiyenera kulowerera pa umoyo wa wina ndi m'nzake tsiku lirilonse. Ngati inu mwandiwona kuti ndazikonda ndekha, muyenera kwa ine ndikunena "Mbale, osakhala odzikonda. Zimenezo zipangitsa Yesu kukhumudwa." Ngati inu mundiona ndikunyada chonde ndithandizeni ndipo mundikumbutse kuti Mulungu amatsutsana ndikunyada. Ine sindifuna Mulungu anditsutse! Muyenera mundithandiza ine, chifukwa ine sindingaone kapena kudziwa kuti ndikulakwa nthawi zonse.

Palibe amene angakwanitse yekha. "Limbikitsanani wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku kuti pasakhale wina oumitsidwa ndi kuputsitsidwa." Ichi ndi mbali ofunikira, (ndipo ndi yomwenso siyimveredwa ndi kutsatiridwa ndi anthu pafupifupi dziko lonse), ya moyo pamodzi tsiku ndi tsiku. Iyi ndi njira imodzi ya chifungiliro imene mudakhalira wa nsembe pogwiritsa ntchito mphatso yanu, ndiponso "kazembe wa Khristu, monga ngati Mulungu adayankhula kuzera mwa inu.

Ngati inu muyika mumachitidwe zoonadi izi zimene kunthawi zonse zakhala zili mu Baibulo lanu, mudzadabwa kuona m'mene Yesu adzakhalira chifupi nanu m'zaka ziwiri zikubwerazi kuchokera pano. "Limbikitsanani wina ndi mnzake tsiku ndi tsiku." Khalani olewerana pa ana ndi banja la wina ndi mnzake ndi kutchito komwe "tsiku lirilonse" pitani komweko! Inu muyenera kuleka ndi kutuluka 'mmalo anu abwino ndi awofuwofuwo" ndikupita komweko kumene simukadatero poyamba! Indedi, ine ndikuthandauza INU! :) Chonde, pakuti Yesu! Akuyankhula MAU. "monga a Mulungu" mu miyoyo yathu, kudzera mu machitidwe, chikondi ndi nzeru, tsiku lirilonse. "pamene mubwera pamodzi abale, aliyense ali nawo mawu a chilangizo, salima, ndi chibvumbulutso." Pamene bvumbulutso libwera kwa wachiwiriyo, siyani oyambayo akhale pansi." Pamene mudzayenda mu ichi, muzapeza kuti ena, amene inu mumaganiza kuti ndi a khristu sakonda Yesu monga inu mumaganizira kuti iwo ali. Inu mudzapezanso kuti ena amene mumaganiza kuti ndi ofooka, akulimbira limbira ndi kuchuluka nzeru kuposa kuganiza kwanuko. Njira ya Mulungu imaoneka poyera zinyanga, ndikupanga ofooka kukhala olimba. Ulemerero kwa Mulungu!

Chuma ichi chayikidwa kwa inu. Chiyikeni m'machitidwe chifukwa cha Yesu. Inu muyenera kutathauzira cheni cheni chomwe ukhristu uli kudzera mu zimene Yesu adanena. Inu muyenera kumvetsetsa za utsogoleri ndi mwenimweni chomwe muyenera kukhalira. Khalani moyo wanu tsiku lirilonse, pamodzi limbitsanani wina ndi mnzake, manganani wina ndi mnzake. Thandizanani kukula wina ndi mnzake ndipo kondani Yesu kwambiri mu mausana ndi mausiku amoyo wanu onse. Bwerani ndi kukumana pamodzi pamanso a Mfumu Yesu.

Baibulo ndi loona mnjira iliyonse. Izi ndi zokhudza Yesu ndi omutsatira ake. Izi ndi nkhani za m'mene amawawidwira mtima ndi mmene amaphunzirira kudzera mmakhalidwe awo ndi Mulungu. Ife tikhonza kuphunzira kuchokera munkhani zawo, koma tikhonzanso kuphunzira: pakukumana ndi kuonana ndi Mulungu pamodzi pamoyo wathu wa tsiku ndi tsiku. Mu ichi nafe tili "malembo amoyo." Zolembedwa zonse mu dziko lapansi sizinganthe ife monga m'mene moyo wapamodzi ungatisinthire ife. Zinthu zakuya zomwe tizifuna sizidzafika pansi pa mitima yathu pamene zingawerengedwa kuchokera pa pepala chabe. Pamene tikonza zinthu pamodzi tsiku lirilonse, Yesu aliphunzitsa ife ziphunzitso zakuya zamoyo zomwe sitingaziphunzire kuchokera m'Baibulo, "ngakhale zoonadi ndi eklezia—mpingo." "MOYO umasanduka kuunika kwa anthu."

Moyo siunapangidwe kukhala ngati sukulu ya galamala yomwe timakaphunzirako mfundo zina ndipo kenako kukhulupirira ndondomeko ina kapena zinthu. Malo mwake Mulungu watiyitana ife kukhala amuna ndi akazi a Mulungu chimodzimodzi monga omwe adaliko pasadabwere ife—olumikizidwa kwa Mulungu yemweyo amene iwo adalumikizana naye—okhala m'chikondi chozama monga iwo adaliri. Kuti chimene tichichite kapena kuchikwanitsa, ife tiyenera osati kudziwa momwe iwo amadziwa zokha. Koma tiyenera kumva chimene iwo amamvera, Mulungu ayenera kuti—tenga paulendo onga ngati wawo. Tsono ife titenga ulendo umenewu mukugwiritsa ntchito Mau a Mulungu kumodzi ndi moyo wathu. Ife tiyenda ulendowu ndi misozi m'maso mwathu, ndikuthandizana wina ndi mnzake—mu nthawi yoipa ndi nthawi yabwino—ndi maso athu pa chiyembekezo chathu, Messiah wathu. Ife tikupita chitsogolo, kukhulupilira kuti Mulungu akhala otipatsa wathu, kutithandiza pomwe tikhala pamodzi.

Ngati ife timukonda Yesu ndi kumanga munjira yoyenerera, zipata za ndende sizidzatilaka. Tchimo lidzaphwanidwa. Zofooka ndi matenda adzachilitsidwa. Machimo adzakhululukidwa. Kuleza mtima kudzatengera ambiri kukulapa. Ubale udzamangidwa kapena kubwezeretsedwa, kuposa m'mene mungalingilire mu maloto anu okoma. Mudzawala ngati nyenyezi mu mlengalenga, kuonetsera ubwino wa Mulungu. Ndipo mkwatibwi, Mpingo adzadzikhalitsa tchelu 'Ndipo adzakhala okonzeka pamene Mkwati adzadza!! Amen.

## Funilo la Mulungu…TSOPANO

Tsiku lina ndimaonera pologalamu yina yokhudza Albert Einstein, mumalonje mudali mau amene adanena chinthu china monga, "Mkamodzi kalikonse munthawi zathawi munthu amabwera ndi zimene zimaonaeka dziko ndi maso osiyana ndi kusintha dziko limene iye amakhalamo." Ife tikufuna kuyika chowinda patsogolo pa inu. Khalani inu monga munthu amene aona dziko osati ndi maso achilengedwe, koma kudzera mu maso a Uzimu. Khalani inu olimba kuti mukhale m'modzi mw aanthu amene Aheberi 11 amayankhula. Onani masomphenya a Mulungu a pokhala pa Mulungu mwa Mzimu ndi ulemerero ochuluka. Onani chithunzi mmaso anu amalingaliro, ngati m'mene okhulupirira mubuku la Aheberi adaonera. Iwo adawona mzinda amene omanga ndi opanga wake adali Mulungu, ndipo pamenepo iwo sanakhutitsidwe ndi china chilichose.

Iwo samafuna kubwereranso kumzinda wakale. Iwo adawona chikonzero chakumwamba chilli patali, ndipo ngakhale iwo samachigwira ndi manja awo, ngakhale panthawi imeneyo sakadakhala mu mzindawu umene Mulungu adaupangira iwo, sanali kufuna kubwerera kumbuyo. "Pamenepo, Mulungu sanachite manyazi kuitanidwa Mulungu wawo ndipo iwo, anthu ake."

Chowinda choterochi chilinso pa inu ndi ine. Onani kuzungulira dziko limene inu muli, maka maka "mpingo" umene inu muli ndiponso kulimbika kwake kudzadza inu munjira yoti mpaka inu muvomera kutaya, kapena kuyika zinthu zanu zonse pamoto m'moyo wanu kuti muonenetsetse kuti chowindachi chakwaniritsidwa mu zonse zozungulira inu. Inu muyika moyo wanu pachiswe. Inu muyika banja lanu pachiswe. Inu muyika ntchito yanu pachiswe, inu muyika *chilichonse* pachiswe chifukwa cha Mulungu ndi zolinga zake. Ichi chiyenera kukhala komwe likuchokera. Kuyankhula monga mwa Baibulo ichi ndicho chikhristu chenicheni chomwe chiliko. Iyi simfundo kapen alingaliro lotchuka, koma ku Aroma 4 amati, **"Amene ali ndi chikhulupiriro cha Abrahamu ndi ana a Abrahamu."**

Tsononthawi kapena mpingo uliwonse umene muli, pali ponse pamene muli (dziko kapena pokhala pamene muli napo ndi mupatcha panyumba tsopano) muyenera kukhala osamalitsa kwambiri kuti musavomereze zinthu zina zomwe Mulungu sadzifuna. Musavomereze izo kuchokera paulesi, umbuli wa Mau a Mulungu, olo kapena mukusowa kwa masomphenya kapena mutchimo lomwe pamoyo wa inu nokha lakuphimbani inu kapena lakuzunzani kuti moziwone kuti ndine operewera. Musalore ena omwe ali okhutitsidwa muchilaodikeya kuti akuyendeni pansi kuti mukhale ofunda chabe osati otentha.

Mwina mwake mwagwiritsa ntchito yoti ndinu MUNTHU wamba chabe ndipo mulibe kalikonse muonetse kapena kupereka. Mwina mwake mukuganiza kuti ganizo lanu silofunika chifukwa kuli anthu ambiri anzeru ndi ophunzira kunjaku…… "Tsono inu mungadziwe chiyani?" Ndingofuna ndikulimbikitseni inu kuti aliyense amene inu muli, muli ndi kena kake koti muonetse kapena kugawa. Ngati inu munamufunsa iye kuti atsuke machimo anu, muli nacho china choti mugawe. Khumbilo lake liri kuchokera pa wangono kufikira pa wamkulu kuti munthu aliyense amudziwe iye, akhale mu uphungu ndiponso muchiyanjano ndi iye, kwa tsiku ndi tsiku.

Kamodzi kalikonse munthawi za nthawi munthu amabwera kapena anthu amalowera, amene ali kufuna, kudzaliona dziko



limene amakhalamo ndi kusintha dziko lomwe lawazungulira iwo. Izo ndizo Aheberi 11. Amanena izo ndi zimene Mulungu watiyitanira aliyense wa ife kuti tikhale ngati tili akulimbika ndi akufuna ndipo muchiyanjano ndi mutu. Khalani mwa iye, ndi pamenepo padzakhala zipatso zambiri zoti tionetse. mukhonza kukhala munthu amene mungathe dziko limene mukhalamo.

Ndili ndi chiyembekezo kuti ife takonzapo kusamvetsetsa pangono kumene kumaononga chikristu icho ndi kuti kusanduka m'khristu ndi pothera nkhani. Ndipo kenako "kukhala nawo mumpingo wakukhosi kwanu pa sabata" ndikukonzanso mpakana Yesu abwerenso ndipo inu kupita kunyumba yanu pamwamba pa phiri. Ine ndikungofuna kuthetserathu maganizo amenewo chifukwa chakuti simaganizo a Mulungu. Mulungu amatcha machitidwe amenewo chipembedzo chabodza ndiponso Laodikeya amene amamusokoneza iye.

*"Cholinga cha Mulungu ndi chakuti tsopano, kudzera mu mpingo, nzeru za Mulungu zidziwike ku ulamuliro ndi amaundido kumwamba..." Aefeso 3:10.*

Ichi ndi cholinga cha Mulungu TSOPANO. Funilo lake ndi kupanga nzeru zake kuti zidziwike **kudzera ku Mpingo.** Osangoti kudzera kwa iwo okha amene amadziona kuti ndi opulumutsidwa, ndiponso osati kungodzera mwa anthu ena ochepera mphamvu amene amamvetsera ku mayankhulo patsiku lina lake la m'sabata atavala masuti ndi mataye…koma kudzera mu umoyo opangidwa, kudzera mugulu la okhulupiriia amene ali "omangidwa ndi kulukidwa pamodzi ndi minofu yogwirizana," ndi anthu amene mphatso zawo ndi zolowerana ndi kulukidwa bwino amene ndi ziwalo za wina ndi mnzake" "mtima umodzi, malingaliro amodzi ogwirizana" Limbanani kuti mukhale ndi masophenya mu machitidwe a okhulupirira osati odzikundikira zolowa, omangiririridwa pamodzi odzipereka kudziphunzitso za atumwi, kunyema mkate chiyanjano, pemphero, tsiku ndi tsiku pachigulu kuchokera pakhomo lina kufikira pakhomo lina. "chipembezo chomangokhala nawo" chilli bwino kwa a Hindu ndi a Silamu, koma sichimene Yesu adayamba ndi kudzodza.

Cholinga chake ndi "kudzera ku Eklezia tsopano," kudzera mulumikizo weniwene ndiponso osati chigulu cha anthu amene amakhala nawo pa china chake, koma miyoyo imene ili yolukana—"Kuvomereza tchimo kwa wina ndi Mnzake," "kunyamulirana chiphinjo cha wina ndi mnzake." Ndiponso "kukondana wina ndi mnzake." Kuti anthu onse adziwe kuti ichi ndichochoka kumwamba (Yohane 13). Iye adati ichi "chidzanyazitsa maulamuliro ndi mphamvu" chifunilo cha Mulungu tsopano "Ndikudzera mu mpingo" kuti uchititse manyazi satana ndi maulamuliro ndi mphamvu zake zonse. Ndipo chifunilo chaka kutengera ndi malembo, TSOPANO ndi kudzera mu mpingo ku apanga adani ake kukhala chopondera cha miyendo yake-osati chabe pakubwera kwake kwachiwiri ndi ufumu wamphamvu wamuyaya chabe, kumene kudzakhale kumaliza kwa ntchito ya Mulungu koma ***TSOPANO.***

Ndiponso, izi ndi zoona, ife sitikuyankhula nkhambakamwa. Ife sitikuyankhula zochita zayendera chigulu, osatinso zokhudzana ndi meleniamu ino, osatinso zokhudzana ulamuliro wa chipembedzo. Osati kufewetsa mafupa ndi minofu yathu, koma mtanda…. Tikuyankhula zokhudza anthu kuwonetsera moyo chimodzimodzi njira imene Yesu adawonetsera moyo wake, ngati Mfumu ya mafumu onse. Iye adabadwa ngati mwana wosabadwira m'banja lokwanitsa mu chodyera cha ng'ombe, amakwera bulu abwereka, ndipo adalibe cholowa (chuma) chenicheni cha iye mwini—opanda mphamvu, maphunziro, opanda "kukongola kapena ulemerero akuti wina aliyense akadakopedwera kw aiye. "Tikuyankhula zokhudza kukhala okonda anthu kuchoka okonda anthu kuchoka pansi pa mtima amene akhonza kuona m'mitima ya anthu ndikuwabweretsa iwo ku mtanda. Tikuyankhula zokhudza kuwaonetsa anthu zokhudza kubwera kwake padziko ndi umoyo wake, ndi kuwayitana iwo akhale asodzi a anthu. Kuti akhale gawo la Nyumba yake, "mokhalamo" mwake. Kuti akhale miyala ya moyo. Omwe sadakhalapo anthu, kukhala anthu." uwu ndiye mtima wa Mulungu.

Landirani Yesu waku Nazareti ndi mfumu "osati wa dziko lino," osati ngati ogonjetsa a Roma kapena dziko lina lirilonse lomwe



timakhalamo, kapena 'mpingo" mlandileni iye ngati mfumu yomwe idakonda, ndipo idakhululukira ndipo idapereka moyo wake……ndipo yomwe idali ndi funilo lotembenuza matebulo ndi kukwapula, ngati padali pofunika, chifukwa chachikondi cha Atate ndi Nyumba ya Atate Ake.

Yesu anali wakufuna kulifunsa dziko limene amakhalamo ndipo pakutero ndi kulisintha ilo, ndipo iye watiyitana ife kukhala chimodzimodzi iye. Uwu siuthenga ungoulutsa. Uwu ndi muyitano kuchiyero ndi kupatulitsidwa ku cholinga cha Mulungu, ndipo uwu ndi muyitano kukweza masomphenya ake mu mtima ndi miyoyo yathu. Gwadani pa maondo anu ndi mupemphere. Uwu ndi muyitano osati ongosintha dziko lowoneka chabe, komanso kusintha dziko losawoneka. "cholinga chake *tsopano,* ndikudzera ku Mpingo kupanga nzeru zake, nzeru zake za Mulungu ku maulamuliro ndi mphamvu" ndi kwa anthu anse.

*"Tsono siyani khala la moto liyeletse milomo ndi mtima wanu, yanganani kwa Mulungu ndi kufuula "ine ndili pano nditumeni!"*